


CHISINDIKIZO CHACHINAI

 Usiku wabwino. Ife tiweramitse mitu yathu tsopano kamphindi chabe kwa pemphero.

² Atate athu Achifundo ndi Akumwamba, ife tikuyandikira Inu kachiwiri usiku uno, tsopano, mu Dzina la Ambuye Yesu, kuti tikupatseni Inu kuthokoza chifukwa cha tsiku lina. Ndipo ife tikupempha tsopano madalitso Anu pa msonkhano usiku uno. Mulole Mzimu Woyera ubwere ndi kutipatsa ife kumasulira kwa zinthu izi zimene ife tikuzifuna molimbikira. O Mulungu, izo zitakhala zopambana chotero kuti ife tikhoza tonse kuyanjana pozungulira Mawu mwa njira yotero, kuti, pamene ife tichoka, ife tidzakhoze kukhala tikunena, “Kodi mitima yathu siyinatenthe mkati mwathu pamene Iye amalankhula kwa ife motsatira njira?” Ife tikukuthokozani Inu pa chimene Iye wakhala ali kwa ife, ndipo kudalira kuti Iye adzatsalabe nafe pamene ife tikupitiriza ulendo, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

³ Wokondwa kwambiri kuti tabwerera mu nyumba ya Ambuye, usiku uno, mu msonkhano kachiwiri! Ndipo ife tiri okondwa. Ine ndiri wokondwa kwambiri kuti . . .

⁴ Ndimangoganiza kuti Chimodzi ichi sichikanabwera, koma Icho potsiriza chinatero. Ndipo kotero ine ndiri wothokoza kwambiri, kuti pokhala chotsiriza cha okwera pakavalo anai awo, chimene ine ndikuganiza chiri chimodzi mwa Mawuthenga aakulu kwa Mpingo pa nthawi yino.

⁵ Ine sindikudziwa chomwe Chimodzi chinacho chiri. Ine ndikungotenga izo tsiku ndi tsiku, basi monga Iye akuwululira Izo. Ine ndikuyesera ku—kupereka Izo, mwa . . . monga Iye aperekerera Izo kwa ine.

⁶ Kodi inu mukasangalala nalo—nalo dalitso? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mwazindikira momwe Izo chabe, mogwirizana nayo mibadwo ya mpingo iyo, basi momwe Izo zikungwirizirana chimodzimidzi mwangwiwo chabe nayo iyo? Ndimo momwe izo . . . Kwa ine, icho chikutsonyeza kuti ndiwo—ndiwo Mzimu Woyera womwewo umene unapereka mibadwo ya mpingo, Mzimu Woyera womwewo ndiye ukupereka Izi, inu mukuwona, chifukwa izo zikugwirizana palimodzi; zonse kuchita kumodzi kwakukulu kwa Mulungu, kudzisonyeza Yekha mu njira zosiyana.

⁷ Inu mukuzindikira, pamene Iye anadzisonyeza Yekha kwa Danieli, mu masomphenya, apo pakanakhala kuyimira kwa chinthu chimodzi, monga m—mbuzi mu malo awa, kapena mwinamwake mtengo; ndipo malo otsatira chikanakhala fano. Ndi—ndi—ndi zinthu zomwe Iye anachita, kuchipanga icho,

chinthu chomwecho nthawi zonse, kungokhala otsimikiza kuti tisaziphonye izo.

⁸ Tsopano, ine ndinali ndithudi wokomedwa mphindi pang'ono pokha zapitazo, ine ndikulankhula kwa dona wamng'ono wakhala apa, pafupi zaka makumi asanu ndi atatu mphambu zisanu zakubadwa. Ndipo iye. . .

⁹ Osati kale, chabe ndisananyamuke kupita cha kumadzulo, bwanji, uko kunali m—msungwana wamng'ono ku mtunda mu Ohio, amene anali, ine ndikuganiza choncho, amene anali kumwalira nayo siteji yotsiriza ya leukemia. Tsopano, leukemia ndi khansara moyenda magazi. Ndipo, o, kanthu kakang'onoko kanali, inu mukudziwa, mchikhalidwe choyipa chotero, mwakuti apo panalibe chiyembekezo china kwa iye nkomwe. Iwo anali kumudyetsera iye mu mitsempha, oparesoni. Ndipo kotero iwo anali kwenikweni banja losawuka. Ndipo iwo. . .

¹⁰ Akazi a Kidd, apa, ndi M'bale Kidd, iwo anawawuza awo za Ambuye woyankha pemphero mochulukwa kwambiri. Ndipo iwo anafika pamodzi, ine ndikuganiza, ndipo analemba ganyu winawake, ndipo anamubweretsa msungwana wamng'ono kumusiko. Ndipo iye anali msungwana wamng'ono wokongola kwambiri, pafupi, o, zisanu ndi chimodzi, zaka zisanu ndi ziwiri zakubadwa. [Mlongo ati, “Zaka zisanu ndi zinai.”—Mkonzi.] Zaka zisanu ndi zinai. Ndipo—ndipo iye anali atabwerera mu chipinda umo. Ndipo. . .

¹¹ Ndipo pamene ife tinapita pamaso pa Ambuye, Mzimu Woyera unapereka mawu kwa iye. Ndipo iwo amayenera kumutenga iye, ndipo amayenera kumutenga iye ndi kumudyetsa iye, inu mukudziwa, mwanjira iyo. Ndipo pamene iye anachoka, iye anali kulirira chitumbuwa, ndipo, kotero, kudya chakudya chake ndi pakamwa. Ndipo iwo anamupatsa iye chitumbuwa chake, ndipo anangopitirira kumudyetsa iye mwachirengedwe.

¹² Mu kanthawi kakafupi, masiku ochepa, iwo anamutengeranso iye kwa dokotala. Ndipo iwo. . . Adokotala mophweka basi sanakhoze kumvetsa. Iye anati, “Monga icho panalibe, ngakhale kuti sanali msungwana yemwe uja.” Iye anati, “Bwanji, apo—apo palibenso ngakhale chisonyezo chimodzi cha leukemia pamenepo, paliponse, paliponse nkomwe.” Kotero, ndipo, iye anali kumwalira. Iwo anali atamulephera kale iye; kumangomudyetsa iye kupyolera mmitsempha yake. Iye anali atasanduka kale chikasu. Inu mukudziwa momwe iwo amafikira. Ndipo kotero iwo. . . Ndipo tsopano iye ali ku sukulu, akusewera nawo ana ena, wokondwa basi monga mmene angakhalire.

¹³ Zikundikumbutsa ine za vuto lina la izo. Tsiku limodzi, ine ndinangobwera kwathu, apo panali. . . Ngati

ine sindikulakwitsa, iwo anali kapena a Episcopalia kapena anthu a Presibateria, amene anali atabweretsa msungwana wamng'ono kuchokera ku Kansas. Ndipo madokotala anali atamulephera iye, ndi leukemia. Ndipo iwo anamupatsa iye, ine ndikukhulupirira, masiku anai okhala moyo; iye anali atafika poyipa kwambiri. Kotero iwo anati iwo anatsiriza masiku anai okha amenewo akubwera kuno, kupyola mu makhwawa a chisanu ndi zinthu, podutsa mu dziko, kuti iye adzapemphereredwe. Ndipo agogo aamuna, amawonekedwe abwino zedi, munthu wachikulire, anali wa tsitsi la imvi.

14 Ndipo iwo anali naye iye, kale, masiku awiri, kumusi kuno mu motelo yaying'ono. Ine—ine ndikuganiza iyo siyiri chiyimire uko tsopano, mbali iyi ya Silver Creek. Ndipo kotero ine ndinapita kumusiko usiku umenewo kukamupempherera iye. Iwo unali mmawa kwambiri. Ine ndinabwera mu usiku umenewo, kuchokera kunja kwa mzinda, ndipo ndinapita kumeneko. Ndipo bambo achikulire... agogo amuna anali akuyenda pansi. Ndipo, amayi, akuyesera kusamalira mwanayo.

15 Ndipo pamene ine ndinagwada kuti ndipemphere, Mzimu Woyera unawulula kwa ine chinsinsi chimene chinalipo pakati pa—pa amayi ndi abambo, za chinachake chimene iwo anachita. Ine ndinawayitanira iwo kumbali ndipo ndinawafunsa iwo za icho. Iwo anayamba kulira, anati, “Uko nkulondola.”

16 Ndiye ine ndinayang'ana mmbuyo, ndipo ine ndinamuwona msungwana wamng'onoyo akulumpha chingwe, akupita, akusewera. Ndipo tsopano mwana wamng'onoyo. . . Mwa pafupi nthawi ya masabata atatu, iwo ananditumizira ine chithunzi cha msungwana wamng'onoyo, atabwerera ku sukulu, akulumpha chingwe, ndipo anali wopanda leukemia, nkomwe.

17 Tsopano, tsopano, mawumboni amenewo ali mwamtheradi choonadi chodalirika, mukuwona. Kotero, Mulungu wathu ali weniweni kwambiri, inu mukuwona. Ife timangomutumikira Iye ndi—ndi kumukhulupirira Iye. Ndipo—ndipo ine—ine ndikudziwa Iye ali weniweni.

18 Tsopano, ine ndikuyesetsa mwakukhoza kwanga tsopano, ndipo pamene chinachake, mkati, pakati pathu, chikupanga njira Yake mopyola. Ndipo tsopano ife tiyesa, usiku uno, mwa chisomo cha Mulungu, kuti titenge Chisindikizo Chachinai ichi, ndi kuwona chimene Mzimu Woyera udzakhala nacho choti ulankhule kwa ife, mu Icho.

19 Tsopano ine ndiwerenga c—Chivumbulutso, mutu wa 6, ndi kuyambira nayo ndime ya 7; ya 7 ndi ya 8. Pali nthawizonse ndime ziwiri; yoyamba ili kulengeza, ndipo ndime yachiwiri ili chimene iye anawona.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachinai, ine ndinamva liwu la chachinai—chamoyo chachinai chikuti, Bwera ndipo udzawone.

Ndipo ine ndinapenya, ndipo tawonani kavalo wotumbululuka: ndipo dzina lake amene anakhala pa iye (amene anakhala) linali Imfa, ndipo Gehena anamutsatira. . . iye. Ndipo mphamvu inapatsidwa kwa iwo pa ngodya zinai za dziko lapansi, kukapha nalo lupanga, ndi njala, ndi imfa, ndipo ndi. . . zirombo za dziko lapansi.

²⁰ Tsopano, Ambuye atithandize ife tsopano kuti timvetse Izi. Ndi chinsinsi.

²¹ Tsopano, kuwoneratu pang'ono chabe, kuti tibwerere mmbuyo, monga ife tinachitira mibadwo ya mpingo, okwera awa ndi kumatula uku kwa Zisindikizo izi. Tsopano, kotero ife tingozitenga izo mmalingaliro athu, kulankhula pang'ono mpaka ife titamverera kuti ndiyo nthawi yoyenera kulankhula.

²² Tsopano, ife tazindikira tsopano, kuti, kumatula kwa Zisindikizo, ndilo Bukhu losindikizidwa la Chiwombolo. Ndiyeno Bukhu liri lokulungidwa ngati sikololo, monga momwe njira yakale inaliri.

²³ [M'bale Branham akuwonetsera kukulungiza ndi kusindikiza kwa sikololo, pogwiritsa ntchito zidutswa za pepala—Mkonzi.] Iyo siyinali buku la mtundu *uwu*; chifukwa ili langobweramo posachedwapa, mabuku a mtundu uwu, mu mapeto, o, ine ndikuganiza zaka zana ndi makumi asanu, kapena chinachake, mazana awiri. Ndiyeno iwo ankayikulungiza iyo, ndiye nkusiya mapeto osamanga. Monga ine ndinakuwuzirani inu momwe izo zinalikuchitikira, ndipo Malemba, poti muwapeze iwo, ndi mu Yeremiya, ndi ena otero. Ndiye otsatira anakulungidwa pamwamba, ndiye mapeto ankawasiya osamanga, ndipo iwo monga *chonchi*.

²⁴ Ndipo chimodzi chirichonse chinali Chisindikizo. Ndipo ilo linali Bukhu losindikizidwa-pasanu ndi pawiri, ndipo ilo linali. . . Palibe mmodzi. . . Pamene iwo anali. . . Ilo linali Bukhu losindikizidwa-pasanu ndi pawiri la Chiwombolo. Ndikhululukireni ine.

²⁵ Ndipo, ndiye, panalibe mmodzi Kumwamba kapena mu dziko lapansi, kapena pansa pa dziko lapansi, anali woyenera kulitsegula Ilo kapena ngakhale kuyang'ana pa Ilo. Ndipo Yohane analira, chifukwa iye sanakhoze kupeza munthu aliyense. . . Chifukwa, ngati Bukhu limenelo silinatengedwe kuchokera mdzanja la Mwini wapachiyambi. . . Kumene, Ilo linali litatayidwa ndi Adamu ndi Eva, ndipo linabwerera, atha iwo kupinyolitsa mawufulu awo a Mawu, malonjezo, cholowa chawo.

²⁶ Iwo, kumbukirani, iwo akulamulira dziko lapansi. Iye anali—iye anali kamulungu kakang'ono, pakuti iye anali mwana wa Mulungu. Ndipo mwana wa Mulungu ali ka—ka—kamulungu

kakang'ono. Tsopano, zimenezo siziri zosiyana kwa Lembu. Ine ndikudziwa kuti izo zikumveka mwachirendo.

²⁷ Koma Yesu anati, “Ngati inu mukuwatchesa iwo, amene Mawu a Mulungu anafikirako. . .” Ndipo Mawu a Mulungu amafikirira kuti? [Osonkhana ati, “Aneneri.”—Mkonzi.] Aneneri. “Ngati inu mumawatchesa iwo, amene Mawu a Mulungu amafikirako, ‘milungu,’ inu munganditsutse Ine bwanji pamene ine ndikuti Ine ndine Mwana wa Mulungu?” Mukuwona?

Ndipo, tsopano, iwo anali milungu.

²⁸ Ndipo munthu, ngati iwe ukhala utabadwa mu banja la dzina la banja lako, iwe ndiwe mwana wamwamuna, ndi gawo la abambo ako.

²⁹ Ndiyeno—ndiye pamene tchimo linalowa mkati, ife tinapeza kuti munthu anawoloka phompho. Ndipo—ndipo magari a ng’ombe ndi mbuzi, ankaphimba, koma sankachotsa. Mpaka, Bulitchi yeniyeni inabwera, imene ikanakhoza kuchotsa banga la tchimo ndi kuliswa ilo kwathunthu mu zidutswa, ndi kulitumiza ilo mmbuyo kwa msokonezi wake wapachiyambi, ameneyo anali Satana.

³⁰ Pamene ilo linabwerera kwa Satana, iye akuyembekezera nthawi yake ya kuwonongedwa Kwamuyaya. Tsopano, izo zikusonyeza zimene ife timakhulupirira. Ife timakhulupirira kuti iye mwamtheradi adzathedweratu kwathunthu ndi kuwonongedwa.

³¹ Ine ndikukhulupirira kuti tchimo lidzaswedwa. Ndipo pamene ilo lavomerezedwa, pa maziko a Magazi a Yesu Khristu, ziri monga kugwetsera dontho la inki yakuda mu bulitchi yambiri ya Clorox. Iyo imangoliswa ilo mpaka kukhala mapulusa, ndi kulitumiza ilo kutali mmbuyo kumene ilo linachokera. Mwawona? Ndipo ndi momwe Magazi a Yesu Khristu amachitira.

³² Ndiye, izo zimamuyika munthu kutsidya kwa phompho kachiwiri, monga mwana wa Mulungu. Mwawona? Ndiyeno iye—ndiye iye amakhala a—a. . . Bwanji, ngakhale iye. . . Mphamvu yolenga ya Mulungu ili mwa iye. Ndipo, mwinabe, pamene Mulungu angakhoze kulamulira icho kuti chichitike, icho chidzachitika. Ndipo ife tikubwerera. Kuti pamene a—a. . .

³³ Mose, pansu pa magari a ng’ombe; ndipo pamene iye anakumana nako Kuwala uko, Lawi la Moto mu chitsamba choyaka chija. Ndipo iye anayima, pansu apo, pa kutuma kumene Mulungu anali atamupatsa iye. Ndipo iye anali mneneri. Ndipo pamene Mawu a Ambuye anabwera kwa iye, iye analankhula, ndipo ngakhale zinthu zinalengedwa mwa Mawu. Mwawona?

³⁴ Tsopano, ngati izo ziti zidzachte izo pansu pa izo, magari a ng’ombe, bwanji Magazi a Yesu? Osati linaphimbidwa; koma kulichotsa ilo, palimodzi. Ndi inu kuyima mu Kukhalapo

kwa Mulungu, monga mwana wowomboledwa. Tsopano, onani, Mpingo wapyola kutali muyeso wake wa kakhaliidwe. Ndipo ine ndikuganiza, nthawi zambiri zochulukuka, ife tikufufuza mmalo mongotulukuka kwenikweni ndi kukumana nalo vutolo.

Ine ndiri nacho chinachake ine ndikufuna kuchinena, ndipo ine—ine nditero pa nthawi yake.

³⁵ Ndipo tsopano zindikirani kuti pali chinachake cholakwika penapake mu mipingo. Ndipo ine ndikuganiza ndiwo machitidwe a chipembedzo amene apiringiza malingaliro a wanthu, ndi zina zotero, mpaka iwo sakudziwa momwe angachitire izo. Uko nkulondola.

³⁶ Koma ife talonjezedwa kuti Izo zikanadzawululidwa. Ndipo tsopano pali Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri zomwe Bukhu ili lasindikizidwa nazo. Ndipo Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izo tsopano. . .

³⁷ Ndiyeno zitatha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izi kutsirizidwa, ife tikupeza, mu Chivumbulutso 10, panali Mabingu asanu ndi awiri achinsinsi amene Yohane anatimidwa kuti alembe, koma ndiye anakanizidwa kuti awalembe amenewo. Ndipo pa nthawi ya Mabingu amenewo, ife tikumupeza Khristu, kapena, “Mngelo akubwera pansi ndi utawaleza, ndipo akuponda phazi Lake pa mtunda ndi pa nyanja, ndipo analumbira kuti nthawi inali itatha, pa nthawi imeneyo.”

³⁸ Ndiyeno ife tikupeza—tikupeza apo, kuti mu kuwulula kwa Zisindikizo, kuti m—Mwanawankhosa anali atasiya ntchito Yake ya ukhala pakati monga Wotetezera, ndipo anali atatulukira tsopano kudzatenga mawufulu Ake, zonse zimene Iye anali atawombola mwa imfa Yake.

³⁹ Ndipo, ndiye, panalibe mmodzi akanakhoza kutsegula Bukhu. Panalibe mmodzi analimvetsa Ilo. Ilo linali Bukhu la Chiwombolo. Ndipo Mulungu Atate, Mzimu, anali nalo Ilo mu dzanja Lawo, chifukwa Khristu anali ali pa Mpandowachifumu monga Mkhalapakati, Mkhalapakati yekhayo. Chotero, apo sipakanakhoza kukhala woyera, popanda Maria, popanda Yosefe, popanda kanthu kalikonse, pa guwa limenelo, chifukwa anali Magazi. Ndipo Magazi wokha a Yesu akanakhoza kupanga chitetezero, kotero palibe china chirichonse chikamakhoza kuyima monga Mkhalapakati. Uko nkulondola. Apo panalibe kanthu kalikonse.

⁴⁰ Kotero lingaliro lonse ili la kutetezedwa naye Yuda mu ndale, ndi kutetezedwa naye Cecilia Woyera mu chinachake chotero, ndizo zamkhutu. Ndicho osati. . . ine—ine sindikuti anthu amenewo sali owona mtima ndi odzipereka. Ine sindikuti inu simuli odzipereka mwa inu pochita izo, ngati inu mumachita. Koma, inu muli kulakwa, inu muli—inu muli odzipereka molakwika. Ndi chirichonse. . .

41 Iwo amati, “Chabwino, uyu—Mngelo uyu, uyu—uyu anawonekera kwa Bonifa Woyera ndi kunena *izi, izo*, ndi *zimzake*. Ndipo iwo ayenera kunena *izi*.” Ine sindikukayika zimenezo pang’ono, mu malingaliro anga, koma kuti wina anawona masomphenya. Ine—ine sindikukayika koma kuti Joseph Smith anawona masomphenya, koma izo sizinali molingana nawo Mawu onse. Kotero choncho, kwa ine, ziri zolakwika. Mwawona? Izo ziyenera kubwera ndi Mawu ena onse.

42 Ndimo momwe mibadwo ya mpingo, ndi Zisindikizo, ndi zina zonse za Izo. Ndipo pamene aliyense aganiza kuti ali nawo Mabingu Asanu ndi awiri awo, ngati izo sizikugwirizana nawo Mawu onse, pali chinachake cholakwika. Mwawona? Izo ziyenera kubwera, PAKUTI ATERO AMBUYE, pakuti *Ili* liri Bukhu. *Ili* liri Vumbulutso la Yesu Khristu, mu uthunthu Wake.

Tsopano, ine—ine ndikukhulupirira ndiye kuti Mwanawankhosa anatulukira.

43 Iwo sanadziwe. Yohane anali kulira. Iye sakanakhoza kupeza aliyense, Kumwamba, pa dziko lapansi, chifukwa onse anali kumbali yina ya phompho, mukuwona, tchimo. Apo panalibe munthu . . . Ndipo Mngelo, zedi, Iye akanakhala woyenera, koma, zitachitika zonse, iye anayenera kukhala Wachibale. Anayenera kukhala munthu wokhalapo. Ndipo apo panalibe chinthu chotericho, chifukwa munthu aliyense anali atabadwa mwa kugonana.

44 Zikanatengera Iye Mmodzi wobadwa popanda izo. Kotero Mulungu Mwiniwake anatenga izo, mu kubadwa kwa namwali, ndi kukhala Emanueli. Magazi Ake anali Amodzi amene anali oyenera. Ndiye pamene Iye anawoloka phompho ili, Iyemwini, ndipo analipira mtengo ndi kukhala mulato wa njira ya ife tonse, ndiye Iye anakhala pansu, kuti akhale Mkhalapakati. Ndipo Iye wakhala ali kukhala pamenepo.

45 Ndipo Bukhu lakhala kwenikweni litatsekedwa, nthawi yonse iyo. Liri pamenepo, koma Ilo likadali mu zophiphiritsa. Iwo analiwona Ilo. Ngakhale Yohane analiwona Ilo. Kulengeza, pamene woyamba anatulukira, iye anati, “Kavalu woyera anatulukira; iye anali naye wokwera pa iye; anali nawo uta mu dzanja lake.” Ndicho chophiphiritsa. Icho sichiri chowululidwa. Ayi. Icho ndi chophiphiritsa chabe. Ndipo, monga munthu aliyense pa dziko lapansi, ndicho chonse iye akanakhoza kunena. Uko nkulondola. Iye akhoza kuphunthwa ndi kuzandima, nzosakayikitsa, kugunda penapake *apa* kapena *apo*, ndipo patapita kanthawi.

46 Koma ife tikupeza, ndiye, kuti mu Bukhu la Chivumbulutso, “Pa Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, zinsinsi (zinsinsi zonse za Ilo) ziyenera kuwululidwa kale pofika nthawi imenoyo.” Tsopano, ndicho Chivumbulutso 10:1-7, kuti Ilo

liyenera kuwululidwa molingana nayo nthawi imeneyo, pa nthawi imeneyo pamene Iye anachita.

⁴⁷ Ndiye Mabingu Asanu ndi awiri analankhula maliwu awo achilendo, ndipo Yohane ankati alembe. Koma, Yohane anadziwa chimene Izo zinali, koma iye—iye sanalembe Izo chifukwa iye anakanizidwa kuti alembe Izo. Ndicho mwamtheradi, ndipo palimodzi, chinsinsi. Izo siziri konse mu chophiphiritisa kapena kanthu. Ife tikungodziwa Iye... Iko kunagunda, ndizo zonse.

⁴⁸ Ndipo tsopano mu kuwerenga izi tsopano, musati muyiwale, tsopano, Lamlungu, kapena Lamlungu mmawa, ife tadumphama msonkhano wamachiritso chifukwa chakukhala nawo mayankho kwa k—kwa mafunso a wanthu. Tsopano, ine ndikufuna inu mukhale nalo funso pa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izi, ngati izo zikukusawutsani inu, chinachake chimene inu simukuchimvetsa. Tiyeni tikhale nawo iwo pa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Ndiye ine ndikhoza kudziwa, pofika Loweruka usiku, ngati ali okwanira ku—kuwayankha iwo, kapena ayi, inu mukuwona. Ndiyeno basi tsopano, mungoti, chabwino, za chinthu chinachake, kapena, “Kodi ine ndichite *ichi?*” Kapena—kapena, mwina ndinali nalo loto. Izo, izo ziri zonse zinthu zoyenera, tsopano, kumbukirani. Izo ziri zinthu zoyenera. Koma tiyeni tikhale pomwepo ndi Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Ndicho chimene ife tiri pa icho kumene. Tiyeni... Ndicho chimene—msonkhano wakonzedwera, Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri. Tiyeni tikhale pomwepo ndi Izo.

⁴⁹ Ine ndiyenera kupita kwathu, ndiyenera kukhala nayo misonkhano pang’ono uko kumadzulo. Ine ndidzabwerera kachiwiri ndiye, mwa pang’ono kuposera mwezi kapena iwiri, kapena chinachake chonga icho, ndipo mwinamwake Ambuye adzalola kuti ife tikhoza kukhala nacho chinthu chinachake pa icho, mwinamwake msonkhano wa machiritso kapena chinachake ndiye, kapena chirichonse ife tiri...chirichonse chimene chiri.

⁵⁰ Ndiye ife tiri nawo Malipenga Asanu ndi awiri apa, oti atulukirebe, inu mukuwona. Ndipo izo zonse zikubwera mmenemo, nazonso. Ndi Mbale Zisanu ndi ziwiri, onani, zoti zitsanuliridwe. Kotero, ndipo izo zonse zidzagwirizana momwe umu, koma izo zonse zikadali zachinsinsi.

⁵¹ Tsopano, usiku watha...Ife tinapeza kuti Chisindikizo Choyamba chinatulukira, ndipo wokwera...Ndipo Ambuye... Kotero ndithandizeni ine, ine sindinali kudziwa izo kale. Palibe cha zinthu izi chomwe ine ndinachidziwapo kale. Uko nkulondola. Ndipo ine chabe sindikuzidziwa.

⁵² Ndinangopita kuntunda uko, ndi kutenga Baibulo ndi kukhala pansu, ndi kukhala kumeneko mpaka pamene Icho chifika pomatuka monga choncho. Ine ndinangotola

cholemba changa ndi kuyamba kulemba. Ndi kungokhala pamenepo, mwinamwake kwa maora, mpaka Icho chifika—Icho chitatsirizika.

⁵³ Ndiye ine ndibwerera, ndipo ine ndinapeza, pamene ine ndikuwona pamene Iye ananena Ichi. Ine ndinaganiza, “Chabwino, zikuwoneka ngati ndinawonapo izo penapake.” Ine nditenga ndemanga zanga, kupita kukayang’ana mmbuyo. “Kodi pali chinachake chonga Icho? Ndipo apa Icho chiri pomwe *apa*. Ndiyeno apa Icho chiri cha *apa* naponso. Ndipo apa Icho chabwerera *apa*, ndipo mmusi *apa*, ndi cha *apa*.” Ndiye ine ndimangozimangiriza Izo mkati. Ine ndikudziwa ameneyo ali Mulungu, malingana ngati Izo zikufanana Lemba ndi Lemba. Ndimomwe Izo ziyenera kuchitira. Monga ngati kumanga nyumba palimodzi, miyala iyenera kukwanira, mwala ndi mwala.

⁵⁴ Tsopano, usiku watha ife tinali nako kutsegula kwa c—Chisindikizo Chachitatu. Choyamba chinali kavalo woyera, ndipo chotsatira chinali kavalo wofiira, ndiyeno kavalo wakuda. Ndipo ife tikupeza kuti okwera anali wokwera yemweyo, nthawi zonse; ndipo ameneyo anali wotsutsakhristu, kuyamba ndi kuyamba. Iye analibe—analibe korona, koma iye analandira mmodzi kenako. Ndiyeno ife tikupeza kuti ndiye iye anapatsidwa lupanga, kuti achotse mtendere pa dziko lapansi, ndipo ife tikupeza kuti iye anachita izo. Ndiye iye analowa umo ndi miyambi ya kupereka, mpingo ndi ndalama, poyeza rupiya kugula *ichi*, ndi marupiya awiri kugula *icho*. Koma iye analetsedwa kukhudza Mafuta ndi vinyo, zomwe zinali pang’ono zomwe zinatsalira.

⁵⁵ Ndiyeno ife tinapereka, tinasiyira usiku watha, ndi kuwonetsera kwa zomwe Mafuta ndi vinyo zinali, ndi mphamvu yomwe Izo zinali nayo. Ndipo ife...Izo mwina zinamveka mwamwano pang’ono, koma ine...izo ziri chabe Chowonadi chimodzimodzi. Mwawona? Tsopano, ife tinasiyira pa...Tiyeni, mphindi pang’ono chabe, kuyang’ananso kwa izo tsopano. Ndiyeno ife tinalekezera, pa mphamvu ya vinyo, chimene Mafuta ankayimira, Mzimu. Tsopano, ine ndikuganiza inu nonse munalembe zonse izo. Inu mudzazipeza izo pa tepi, ngati inu simunatero. Ndi pamene mungawapeze Malemba, kuti, mafuta nthawizonse amayimira Mzimu Woyera. Monga anamwali opusa opanda Mafuta, anamwali ochenjera anali nawo Mafuta, amene ali Mzimu Woyera. Ndiyeno mpaka mmbuyo, mu—mu—aneneri, ndi ena otero. Ndipo tsopano ine... .

⁵⁶ Zedi, ine sindikuyesera kusolola Lemba lililonse mmenemo. Ndipo pali zinthu zomwe iwe sungakhoze ngakhale kuzilankhula; zotenga nthawi yochuluka kwambiri. Koma ine ndikuyesera kuziyika apa, ndi Malemba ndi zina zotero, zokwanira basi kuwapatsa anthu kotero ziwalole iwo kudziwa ndi kuwona chithunzi cha Izo. Koma ngati iwe ukanakhala

pansi ndi chimodzi cha Zisindikizo izo, bwanji, mai, iwe ukhoza kutenga maulaliki amiyenzi usiku uliwonse, kumene pa Chisindikizo chimenecho, ndipo komabe nkusachikhudza Icho nkomwe, mwawona, pa chimodzi cha Izo. Ndipo ndimo momwe—kuchuluka kwake ziri kwa Izo. Koma, kugunda chabe malo a pamwamba a Izo, ndiye iwe ukhoza—iwe ukhoza kuwona chomwe Izo zonse ziri.

⁵⁷ Tsopano, monga mafuta ankaphiphiritsira Mzimu Woyera. Ndiye ife tikupeza kuti mafuta ndi vinyo ziri zolumikizana mu kupembedza, onani, nthawizonse zolumukizana mu kupembedza.

⁵⁸ Ndipo vinyo, ine ndinati, chimene chinabwera kwa ine, kuti vinyo amaphiphiritsira kuti inali mphamvu ya—inali mphamvu ya kukondoweza mwa vumbulutso. Mwawona? Ndipo apo ndi pamene chinachake chawululidwa. Icho chimapereka kukondoweza kwa wokhulupirira, chifukwa icho chaperekedwa mwa vumbulutso. Mwawona? Ndicho chinachake chimene Mulungu wanena. Ndicho chinsinsi; iwo sangakhoze kumvetsa Icho, onani. Ndipo, patapita kanthawi, Mulungu amabwera pansi ndi kuchiwulula Icho, ndiyeno nkuchitsimikizira Icho.

⁵⁹ Kumbukirani, ngati Chowonadi chawululidwa, Chowonadi nachonso chimatsimikiziridwa. Mulungu, mowirikiza, ziribe kanthu kaya munthuyo ali wophunzira bwanji, kaya akhala wanzeru bwanji mu malingaliro ake; ngati Mulungu sayikira kumbuyo zomwe iye akunena, pali chinachake cholakwika. Mwawona? Kulondola. Chifukwa, iwo ndi Mawu.

⁶⁰ Tsopano, pamene Mose anapita kumeneko pansi pa kudzoza kwa Mulungu, anati, “Lolani ntchentche zibwere.” Ntchentche zinabwera. Anati, “Lolani achule abwere.” Achule anabwera.

⁶¹ Penyani, bwanji ngati iye akanati, “Lolani ntchentche zibwere,” ndipo izo nkusabwera? Mukuwona, ndiye iye—iye sanalankhule Mawu a Ambuye, mukuwona; iye anangolankhula, iye analankhula mawu ake omwe. Iye mwina anaganizira kuti payenera kukhala ntchentche. Koma, apo—apo sipanabwera ntchentche iliyonse, chifukwa Mulungu anali asanamuwuze iye choncho.

⁶² Ndipo pamene Mulungu akuwuzani iwe chirichonse, ndi kuti, “Iwe upite ukachite *ichi*, ndipo Ine ndidzakhala nacho icho, pakuti awa ali Mawu Anga,” ndipo Iye nkuchisonyeza icho mu Baibulo, ndiye Mulungu amayima kuseri kwa icho. Ndipo ngati icho sichinalembedwe mu Baibulo, Mulungu amayima kuseri kwa icho, chonchobe, ngati icho chiri Mawu a Mulungu. Mwawona?

⁶³ Ndiyeno ngati icho chiri kunjika kwa ilo, icho chimawululidwa kwa aneneri. Iye tikuzindikira kuti zinsinsi zonse za Mulungu zimazindikiritsidwa kwa aneneri, ndipo iwo okha. Mwawona, Amosi 3:7.

64 Tsopano, tsopano, mphamvu ya vumbulutso imabweretsa kukondoweza kwa wokhulupirira. Pakuti, mphamvu ya vinyo, vinyo wachirengedwe, ali woti akondoweze. Mwawona? Ali woti—woti abweretse munthu, amene ali wogwa pansi, ku kukondowedwa. Mwawona? Mwawona? Chabwino, ndiye, tsopano, pali mphamvu ya vumbulutso la Mawu, imapereka kukondoweza kwa chisangalalo kwa wokhulupirira, kukondoweza kwa chikhutitso, kukondoweza kuti Iwo avomerezedwa, Iwo atsimikiziridwa.

65 Iwo amatchedwa, mu Lemba, monga ife tikufuna kufanizira kwa ilo, monga “vinyo watsopano.” Ife nthawizonse timafanizira kwa ilo monga choncho, monga, “Awa aledzera naye vinyo watsopano.” Mwawona? Chabwino. Kapena, “vinyo wauzimu,” Ine ndikuganiza, kumasulira kwabwino kukanakhala. Iko kukanakhala, pa “vinyo wauzimu.” Monga vinyo wachirengedwe amadziwulula yekha mu mphamvu yokondoweza, kotero amatero vinyo watsopano, pamene Iye awulula Mawu a Mulungu, umene uli Mzimu. O! Tsopano pali...ndicho... Penyani, Mawu Pawokha ali Mzimu. Inu mukhulupirira zimenezo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

66 Tiyeni tiwerenge izo. Tiyeni tiwerenge izo, Yohane Woyera 6. Tiyeni chabe...Eya, ndiye inu—ndiye inu—inun simunena kuti, “Chabwino, tsopano, winawake ananena izo.” Tiyeni—tiyeni tiwone Yemwe ananena izo, ndiyeno ife tidzidwa ngati icho chiri Chowonadi, kapena ayi. Yohane Woyera, mutu wa 6. Ndipo mutu wa 6, ndipo ine ndikukhulupirira ndiyo sikisite...ndime ya 63, chabwino, ine ndikuganiza iyo ili. Inde.

Ndi mzimu umene umafulumizitsa; thupi silipindula kanthu: mawu amene ine ndilankhula kwa inu, iwo ali mzimu, ndipo iwo ali moyo.

67 Mawu Pawokha ali Mzimu. Iwo ali Mzimu mwa mawonekedwe a Mawu. Ndiyeno, inu mukuwona, pamene Iwo afulumizitsidwa, kapena kubweretsedwa ku moyo, Mzimu wa Mawu umapita ku kukagwira ntchito ndi kuchitapo. Mwawona? Chifukwa kuti...

68 Tsopano penyani apa. Ganizo liyenera kukhala ganizo ilo lisanakhale mawu. Ndiyeno pamene ganizo liperekedwa, ilo liri mawu. Tsopano, *ili* liri ganizo la Mulungu limene Iye waliyika mu Mawu. Ndiyeno pamene ife tililandira Ilo kuchokera kwa Iye, Ilo limakhala Mawu.

69 Mulungu anawulula kwa Mose choti achite. Mose anachilankhula icho, ndipo icho chinachitika. Mwawona? Ndi chimenecho, pamene icho kwenikweni chichokera kwa Mulungu.

70 Tsopano ife tikupeza, kuti—kuti Ilo—Ilo limakondoweza ndipo Ilo limapatsa chisangalalo, chifukwa Ilo liri Mawu a Mulungu. Ndipo vinyo watsopano, vinyo watsopano

amakondoweza... pamene Ilo liwulula Mawu. Ndiye, limabweretsa chisangalalo chopitirira muyezo, nthawizina. Ife tinapita kupyola zimenezo, kuti ilo limabweretsa chisangalalo chotero mpaka iwe umafika posefukira.

⁷¹ Tsopano, ine ndikudziwa apo pali zambiri zotentheka, ndi anthu kumatengeka. Ine ndikudziwa nthawizina iwo amachita izo pamene nyimbo ikulumphalumpha, ndi chirichonse. Ndipo ine ndikudziwa kuti izo zimachitika. Ndipo ine—ine ndimakukhulupirira izo, nanenso. Koma ine ndawonapo anthu mu tsiku pamene, bola ngati nyimbo ikuyimba, aliyense anali kulumpha ndi kumafuwula; koma pamene nyimbo inayima, izo zinayima. Mwawona? Ine ndikukhulupirira... Chabwino, izo, zonse ziri bwinobe, monga mmene ine zikundikhudzira, inu mukuwona, bola ngati anthu akukhala miyoyo yabwino. Ndi...

⁷² Koma, tsopano, chimene, iwe uyamba kubweretsa Mawu! Tsopano, ndicho chinthu chimene makamaka chimabweretsa Moyo, ali Mawu, ndipo iwo amabweretsa chisangalalo cha kukondoweza kwa vinyo watsopano. Mukuwona? Inde. Ndipo ndicho chimene chinali pa Pentekoste, pamene Mawu anatsimikiziridwa.

⁷³ Tsopano penyani. Tsopano, Yesu anawawuza iwo, Luka 24:49, “Taonani, Ine ndituma lonjezo la Atate Anga pa inu; koma inu mupite ku Yerusalemu ndipo mukayembekezere kufikira.” Lonjezo la Atate linali chiyani? Yoweli 2:28, bwanji, ife tikupeza kuti, Iye akuti “atsanulira Mzimu.” Mu Yesaya 28:19, momwe kukanadzakhala “milomo yachibwibwi, ndi malirime ena,” ndi zinthu zina zonse izi.

⁷⁴ Iwo anapita pamwamba paja. Ndipo monga ife tinapyola zimenezo, mwinamwake mmodzi anati, “Chabwino, ine ndikukhulupirira ife tayembekezera kotalika mokwanira. Tiyeni tingolandira icho mwa chikhulupiriro.” Icho chinali chiphunzitso chabwino cha Abapatisti, koma icho sichinagwire ntchito ndi abale awo.

⁷⁵ Kotero ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, icho chinayenera kukhala chenicheni. Ndipo iwo anayembekezera pa utumiki wawo, kuti Mawu atsimikiziridwe. Ndipo pamene iwe ubwera kudzapereka Mzimu Woyera, iwe uchite chomwecho.

⁷⁶ Inde, iwe ukhoza kuwulandira iwo mwa chikhulupiriro. Iwe uyenera kulandira Khristu mwa chikhulupiriro. Ndiko kulondola chimodzimidzi. Ndipo iwe umalandira Mzimu Woyera mwa chikhulupiriro; koma ndiye lola Mzimu Woyera ubwere ndi kudzapereka mdulidwe, monga umboni wakuti Iye wavomereza chikhulupiriro chako, inu mukuwona. Ndiye, onani, “Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo chinawerengedwa kwa iye chilungamo.” Koma Mulungu anamupatsa iye

chizindikiro cha mdulidwe, monga chitsimikizo chakuti Iye anali atalandira chikhulupiriro chake.

⁷⁷ Kotero ndicho chinthu chofanana chimene ife tiyenera kuchita. Ife tiyenera kuyembekezera pa Mzimu Woyera mpaka Iwo utachita chinachake; si koyenera chifukwa ife tinalankhula mu malirime, osati chifukwa ife tavina, kapena tiri nako kutengeka, ife tinafuwula. Mpaka pamene ife tinasinthidwa; mpaka chinachake makamaka chitachitika! Ine sindikusamala kaya iwo ulowamo mwa maonekedwe anji. Chabe kuti izo zachitika, ndicho chinthu chachikulu. Mwawona?

⁷⁸ Ndipo ine ndimakhulupirira kulankhula mu malirime uko ndi zinthu zina zonse izi ziri zabwino, koma kungoti izo pa zokha sizingagwire ntchito. Ndipo inu mukudziwa izo sizingagwire ntchito. Kotero, izo sizimachita icho.

⁷⁹ Ine ndawonapo afiti achikazi akulankhula mu malirime, ndawona afiti achimuna akulankhula mu malirime ndi kuvina mu mzimu. Ndithudi. Kuyika pensulo pansu ndipo iyo nkumalemba mu malirime achirendo. Ndipo wina nkumasulira izo, uko nkulondola, ndi kumanena zowona. Uko nkulondola. Atalemba chimodzimodzi kumene zomwe zinali zitachitika, ndipo izo zinali basi chimodzimodzi mwanjira imeneyo. Kuwawona iwo akuponyeza fumbi pa mutu, ndi kudzidula okha ndi mipeni, ndi kudziphimba ponse ndi magari a chinyama chakuthengo kapena chinachake, ndipo—ndipo, ndithudi, onani, ndi kuyitanira pa Mdierekezi. Kotero, inu mukuwona, izo siziti . . .

⁸⁰ Kulankhula mu malirime sikuchita icho. “Ngakhale ine ndilankhule ndi lirime la anthu ndi Angelo, ndipo ndiri wopanda chikondi, izo sizindipindulira ine kanthu. Onani, ngakhale ine ndingakhoze kuchita izo!” Mukuwona? Kotero zinthu izo sizimatanthawuza kuti inu muli nawo Mzimu Woyera.

⁸¹ Koma pamene Iye, Munthu, m—Mzimu wachisavundi wa Khristu ukhala Mpulumutsi wanuwanu, ndi kukusinthani inu, ndi kuponyera malingaliro anu molunjika kumene ku Gologota ndi ku Mawu awa, chinachake chachitika. Inde, bwana. Chinachake chachitika. Palibe mmodzi adzasowe kukuwuzani inu za icho. Inu mudzachidziwa icho pamene icho chichitika.

⁸² Ndipo vinyo watsopano, pamene iye abweretsa vumbulutso, ndiye Iwo—Iwo awululidwa.

⁸³ Ndipo ndimo momwe zinaliri pa Pentekoste. Iwo anadziwa kuti—kuti pankayenera kukhala Mzimu utatsanuliridwa pa iwo, ndipo iwo anayembekezera mpaka ichi chitachitika. Ndipo pamene kutsimikizira kwa vumbulutso kunachitika, ndiye kukondoweza kunali pa iwo. Iwo ndithudi anachita. Iwo anafuka nthunzi, nawonso. Iwo, mpaka panja mmisewu; kumene, iwo ankachita mantha, ndipo ankatseka zitseko. Ndipo iwo anali panja mmisewu; kumene, iwo anali akuchita

mantha nalo gulu la anthu; kulalikirira Uthenga kwa iwo! Uko nkulondola. Mukuwona? Chinachake chinali chitachitika, chifukwa Mawu owona a lonjezo anatsimikiziridwa.

⁸⁴ Tsopano tiyeni tiyimire apa miniti. Ngati icho chinabweretsa kutsimikizika kotero kwa anthu awo, kuti iwo—iwo. . . Pafupi mmodzi aliyense wa iwo anasindikiza umboni wawo ndi magari awo. Ziribe kanthu kaya kunabwera chiyani potsatira, malingana ngati iwo ankakhala moyo, iwo sichinawathere konse Icho. Icho chinakhala pamenepo, chifukwa icho chinali Mawu owona a lonjezo, atatsimikiziridwa. Vumbulutso kukhala lotsimikiziridwa. Ndipo iwo anafa, akusindikiza umboni wawo ndi magari awo omwe.

⁸⁵ Tsopano penyani pa lonjezo la masiku otsiriza. Ndipo apa ife tikuliwona ilo likutsimikiziridwa pamaso pathu pomwe, k—kubwera kwatsopano kwa Mzimu Woyera ndi ntchito zomwe Iye ankayenera kuchita, ndipo ife tikuzipeza izo pakati pathu pomwe. Mwawona? O, ife tiyenera. . . O, mai! Ife tingamve bwanji? Chinachake chimachitika, ine ndikukuwuzani inu, mzanga! Pamene wokhulupirira weniweni, wowona, wodzipereka, wokonzedweratu, pamene Kuwala uko kufika pa mbewu imeneyo, chinachake chimaphulikira ku Moyo watsopano. Mkazi wamng’ono uja pa chitsime!

⁸⁶ Pamene, ansembe ausikolala awo anali atanena, “Chabwino, uyo ndi Mdierekezi. Iye ndi wamatsenga. Iye ali—Iye akuwawuza chabe anthu awo mwayi wawo. Ndipo Iye ali—Iye ndi mdierekezi.”

⁸⁷ Koma, pamene, mkazi wamng’ono uja ndi mbewu yokonzedweratuyo! Tsopano inu mukuganiza kuti uko si kulondola? Koma Yesu anati, “Palibe munthu amene angadze, pokha Atate Anga atamukoka iye; ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera.” Ndipo Iye. . .

⁸⁸ Ndipo wotsutsakhristu, masiku otsiriza, adzakhala wokhoza. . . Mzimu wotsutsakhristu uwo umene ife tikuwuwerenga, mu zazipembedzo, ndipo tinatsimikizira kuti zazipembedzo ziri zotsutsakhristu. Tsopano, kupyola, munthu aliyense akanakhoza kuchoka pano monga choncho, iye, pali chinachake cholakwika, ndipo nkumakhulupirirabe kuti kachitidwe ka chipembedzo sikali kotsutsakhristu. Pamene, mwamtheradi zikutsimikiziridwa, kuchokera ku mbiriyakale, kuchokera ku chirichonse chimene chiripo, mpaka kupyola mu Baibulo la Mulungu ndi china chirichonse, ndi zotsutsakhristu. Ndipo Roma ali mutu wa izo. Ndipo tiana tatikazi ta mipingo tikutsatira konseko. Ndipo onse a iwo akuponyedwa mu gehena. Uko nkulondola. Kotero ife tikuwona chinthu ichi, chotsutsakhristu, mzimu wa izo.

⁸⁹ Ndipo tsiku limene ife tikukhalamo, ndipo, bwanji, ilo liyenera kubweretsa “chimwemwe chosasimbika ndi chodzaza

ndi ulemerero.” Mkazi wakale wamng’ono uja, mwamsanga pamene icho chinamukhudza iye, mai, mbewu inatulukira!

⁹⁰ Tsopano, kumbukirani, Baibulo limanena, kuti mu tsiku lotsiriza, kuti wotsutsakhristu uyu akanakhodza “kunyenga dziko lonse.”

⁹¹ Apo pakanadzakhala chiwerengero chaching’ono chokha, amene maina awo anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa asanayikidwe maziko a dziko. Ndipo pamene kutsimikizira kowona uko kwa Chowonadi chowululidwa cha Mawu a Mulungu kukhudza mtima umenewo, iye akhudza madzi, ndipo mpaka kutsidya ndi Mzimu Woyera, basi molimba momwe iye angathere. Ndipo inu simungamuyimitse iye kuchita izo, chifukwa Moyo watsopano unagwira ntchito.

⁹² Ine ndinali kulankhula kwa munthu, osati kale lapitalo, anali kuyesera kukambirana nane, ndipo amati, “Kodi iwe sukuchita manyazi kunena kuti ‘Mulungu analenga miyamba ndi dziko lapansi mu masiku atatu . . . kapena mu masiku asanu ndi limodzi?’”

Ine ndinati, “Ndicho chimene Baibulo linanena.”

⁹³ Anati, “Chabwino, ife tiri nawo umboni ndipo tikhoza kutsimikizira kuti dziko liri zaka mamilioni liripo.”

⁹⁴ Ine ndinati, “Izo zinalibe chochita chirichonse nacho icho. Mu Genesis 1:1, Ilo linati, ‘Pachiyambi Mulungu analenga miyamba ndi dziko lapansi.’ Basi! Ndizo zonse, mukuwona. ‘Tsopano dziko linali lopanda mawonekedwe, ndi lamdima.’” Ndipo ine ndinati, “Ine ndimakhulupirira mbewu iliyonse inali kugona momwemo, kuchokera ku chitukukuko china kapena chinachake. Ndipo mofulumira pamene madzi ananyamulidwapo, ndipo kuwala kunakhudza iyo, pamwamba panabwera mitengo ndi chirichonse.”

⁹⁵ Ndipo chinthu chomwecho ndi munthu wokhalapo, chiri choyimira. Pamene n—n—nkhungu yonse inali itachoka, ndipo Chowonadi chowululidwa kwa mbewu yeniyeniyo ikugona pamenepo, idakali yamoyo, ndipo Kuwala kwa Uthenga kukhoza kukhudza iyo mwa kutsimikizira kowona kwa Mawu, idzakhala moyo. Iyo ili nawo Moyo mkati mwake. Iyo idzakhulupirira. Kunja kwa izo, iyo siyingakhale moyo; iyo ilibe Moyo mwa iyo.

⁹⁶ Mayina awo analembedwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa asanakhazikitsidwe maziko a dziko, adzatulukira basi motsimikiza monga chirichonse. Ndipo ndicho chifukwa chake Yesu akukhala Pamenepo ndi kuyembekezera nayo ntchito Yake ya ukhalapakati, mpaka mbewu yotsirizayo. Ndipo iye adzaziwa chimodzimodzi pamene iko kukukhudza.

⁹⁷ Monga Dr. Lee Vayle . . . ine ndikuganiza iye akadali mu msonkhano penapake. Ine sindinamuwone iye kwa masiku. Ine sindikukhulupirira ine ndinamuwona iye. [M’bale ati, “Iye

ali apa.”—Mkonzi.] Iye ali pano. Chabwino, tsiku lina iye ananditumizira ine pepala ili, la zimene Ireniyasi ananena. Chabwino, ine ndinamutenga Ireniyasi, kuchokera njira yakalekale, kukhala mngelo wa m’badwo umene iye anali. Koma iye anati, “Pamene chiwalo chotsiriza icho cha Thupi chabwera mkati,” mu m’badwo wotsiriza uno, “kuyenera kukhala... chinthu chikanadzawululidwa pa nthawi imeneyo.” Ndipo apa icho chiri. Icho chiri cholondola chimodzimidzi. Mwawona? Ife tiri mu tsikulo. Chabwino.

⁹⁸ Ndiye, Pentekoste anali nacho chisangalalo chopitirira. Iwo anali kwenikweni atakondowededwa. Ine ndikuganiza, icho chimachita aliyense.

⁹⁹ Tiyeni tingotenga kamphindi chabe. Tiyeni tiganize za Davide. Iye—iye anali yense anakondowededwa, nayenso. Iye anati, “Chikho changa chikusefukira.” Ine ndikuhulupirira iye anali nacho kwenikweni c—chochitika chachikulu mu moyo wake. Chiyani, nchiyani chinamupangitsa iye kuchita izo? Pamene iye anali mu Mzimu... Pakuti, iye anali mneneri. Ife tikudziwa iye anali. Baibulo linanena choncho. Mneneri Davide, tsopano, pakuti iye anali mneneri, ndipo iye anali mu Mzimu, ndipo iye anawona chiwukitsiro. Ngati inu mungafune kuwerenga izo, ziri mu Salmo 16:8 mpaka 11. Iye anati, “Komanso mnofu wanga unapangidwa kukondwa. Mai! Ine—ine ndikupumula mu chiyembekezo, chifukwa Inu simudzasiya moyo wanga mu hade; ngakhalenso Inu simudzalola Mmodzi Woyera Wanu kuti awone chivundi.” Ndipo ine ndikukuwuzani inu, chikho chake chinafika posefukira, chifukwa iye anawona. Ziribe kanthu chomwe icho chinali; o, iye anawona chiwukitsiro, ndipo iye anali kwenikweni. . . ndipo chikho chake chinasefukira.

¹⁰⁰ Ndiponso, Davide anali nacho chikho china chikusefukira, mu Samuele Wachiwiri, (pokhala kuti inu mwatulutsa mapensulo anu), Samuele Wachiwiri 6:14. Apo kunali kadanga kowuma.

¹⁰¹ Iwo anali atatenga likasa. Mdani anali atalowa mkati ndi kutenga likasa la Ambuye, ndipo iwo anali atalitsitsa ilo ndi kuliyyika ilo pamaso pa Dagoni, ndipo Dagoni anagwa chafufumimba. Ndipo analitengera ilo ku mzinda wina, ndipo miliri inafalikira. Icho chinali. . . Ilo linali chinthu chotentha kwambiri chomwe iwo anakhalapo nacho pa manja awo, kumusi uko. Ndipo iwo sakanakhoza kulichotsa ilo, chifukwa ilo linali litachoka pamalo ake.

¹⁰² Tsopano, pamene iwo analiyika ilo pa ngolo ya ng’ombe, ndi kuyamba kubwerera. Ndipo pamene Davide analiwona likasa likubwera, inu mukudziwa chimene iye anachita? Iye—iye anadzazidwa kwambiri, ndipo chikho chake chinayamba kusefukira; kukondoweza! Pamene iye anawona Mawu

akuwululidwa kubwerera mu Israeli kachiwiri, iye anavina mu Mzimu, ponse pozungulira, kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, kuzungulira, monga choncho. Eya. Chikho chake chinayamba kusefukira, inu mukuwona. Chifukwa? Iye anawawona Mawu akubwerera.

¹⁰³ Ine ndikuganiza icho chikanamupanga aliyense kukondowededwa pang'ono pamene iwo akuwona, zitatha zaka zonse izi; ndiyeno Mawu owona, mwa lonjezo lakuti iwo akanadzakhala, kukhala akubweretsedwa ndi kutsimikiziridwa. Nthawi yotani! Nthawi yotani!

¹⁰⁴ Tsopano tiyeni tiweringe. Ine—ine ndikuyamba kulankhula konse, ine sindifika ku izi, ndipo ine ndikhala nanu inu nonse muno mpaka hafu pasiti teni. Ine ndinakulolani inu kutuluka mofulumira usiku watha, kotero ine ndiyenera kukusungani inu kwa nthawi yabwino yayitali usiku uno. [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Eya. Eya. Ayi, ine ndinali kungokuserewulani inu. Mukuwona? Ndiri. . .Ife tikungofuna basi mmene Ambuye ati atsogolere tsopano.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachinai, ine ndinamva liwu la chamoyo chachinai chikuti, Bwera. . .udzawone.

¹⁰⁵ Tsopano, “Pamene Mwanawankhosa anali atatsegula Chisindikizo Chachinai.” Tiyeni tiyimire apo tsopano. Chisindikizo Chachinai, tsopano, Ndani anatsegula Icho? Mwanawankhosa. Kodi analipo wina aliyense woyenera? Palibe mmodzi aliyense akanakhoza kuchita izo. Ayi. Mwanawankhosa anatsegula Chisindikizo Chachinai.

¹⁰⁶ Ndipo c—Chirombo chachinai, Cholengedwa chamoyo chonga mphungu, chinati kwa Yohane, “Bwera, udzawone chimene chinsinsi chachinai cha dongosolo la chiwombolo, chakhala chitabisika mu Bukhu ili,” chifukwa Mwanawankhosa anali kutsegula Ilo. Mwa kulankhula kwina, ndicho chimene iye anali kunena. “Pali chinsinsi chachinai apa. Ine ndakuwonetsa iwe, mu chophiphiritsa. Tsopano, Yohane, ine sindikudziwa kaya iwe wamvetsa Izo, kapena ayi.” Koma, iye analemba zomwe iye anawona, koma izo zinali chinsinsi. Kotero, iye analemba zimene iye anawona.

¹⁰⁷ Mwanawankhosa anali kumatula Zisindikizo, ndipo Mulungu anali samawululebe Izo. Izo zinasiyidwira kwa tsiku lotsiriza. Mwawona? Tsopano, ife tinali nazo zophiphiritsa, ndipo ife tatokosa pa izo, ndipo tachita bwino kwambiri nthawizina, mwawona. Koma ife tikudziwa Izo zakhala zikusunthirabe patsogolo. Koma tsopano, mu masiku otsiriza, ife tikhoza kuyang'ana mmbuyo ndi kuwona kumene Izo zakhala ziri. Ndipo izo ziyenera kuchitika, izo, pa mapeto a m'badwo wa mpingo, Mkwatulo usanachitike kumene.

108 Momwe wina angawutengere Mpingo kupita ukupyola mu Chisawutso, ine sindikudziwa. Koma Iwo upyoleranji mu Chisawutso, pamene Iwo ulibe—ulibe tchimo? Ine ndikutanthawuza...ine sindikutanthawuza mpingo; mpingo udzapyola mu Chisawutso. Koma ine ndikulankhula za Mkwatibwi. Mkwatibwi, ayi, Iye alibe tchimo lomutsutsa Iye, nkomwe. Ilo lachotsedwa kale ndi bulitchi, ndipo palibe ngakhale a—a...Palibe ngakhale fungo la ilo, ndipo palibe kanthu katsalira. Iwo ali angwiro, pamaso pa Mulungu. Kotero Chisawutso chirichonse nchachiyani kuti chiwayeretse iwo? Koma enawo akuchita. Mpingo ukuchita kupyola mu Chisawutso, koma osati Mkwatibwi.

109 Tsopano, tsopano ife tizitenga chabe izo mu zophiphiritsa za mtundu uliwonse tsopano. Monga—mpingo, Nowa, mtundu wonyamulidwira pamwamba, anapitirira mpaka mu tchimo. Onani, tsopano, iwo anachita kupita pamwamba. Koma, Enoki anapita poyamba, uwo unali mtundu wa oyera amene akanadzapita mkati, ndipo isanafike nthawi ya Chisawutso.

Tsopano ife tikupeza kuti, Mwanawankhosa uyu anatsegula Chisindikizo.

110 Tsopano, Chirombo choyamba ife tikuchipeza, ngati inu mungazindikire, Chirombo choyamba ife tikuchipeza, chinali a...Chirombo choyamba chinali mkango, Cholengedwa chamoyo; tinapeza izo mu bukhu la zisi...la mibadwo ya mpingo. Ndiyeno Chirombo chachiwiri, ine ndikukhulupirira, chinali—nkhope ya ng'ombe, kapena mwanawang'ombe. Ndipo Chirombo chachitatu chinali nkhope ya munthu. Koma Chirombo chachinai chinali nkhope ya mphungu. Tsopano ndicho chimodzimidzi momwe ife tinapezera izo, zikusuntha chimodzimidzi basi monga choncho. Ndipo ndimo chimodzimidzi momwe izo zayikidwira ngakhale mu Bukhu apa.

111 Ndiyeno monga mphunzitsi wamkulu, pa nthawi yina mu Florida, akuphunzitsa, kunena kuti—kuti...kuti, “Bukhu la Machitidwe linali chabe mwawamba n—ntchito yamiyanga kwa k—kwa Mpingo. Mpingo unayambitsidwa mu Mawuthenga anai.”

112 Ndipo ife tikupeza, zosiyana kwa izo, kuti ali Mawuthenga anai amene akulondera Bukhu la Machitidwe. Ndi kuchokera ku Mawuthenga anai awo kuti Bukhu la Machitidwe lalembedwa, machitidwe a Mzimu Woyera mwa atumwi. Ndipo ife tikupeza, cha mu Bukhu, kuti olondera awo anali kukhala pamenepo akuyang'ana; kummawa, kumpoto, kumadzulo, ndi kummwera. Mukukumbukira momwe ife tinajambulira izo apa? Ndipo momwe kukongola kwake ndi mwangwiro chirichonse chinagunda basi pa malo ake!

113 Tsopano ine ndikufuna inu muzindikire. Anati, “Bwera ndipo udzawone.” Yohane...Tsopano ine ndikufuna inu muzindikire kachiwiri, ichi chisanachitike. Tsopano, ichi apa chiri chotsiriza cha okwera, kuti chiwulule kuchita kwa wotsutsakhristu.

Mawa usiku, tigunda miyoyo ya pansi paguwa.

Usiku wotsatira, ziweruzo.

114 Usiku wotsatira, kupita kwina, kwa—kwa mapeto a m’badwo, mapeto a nthawi, a zinthu zonse, mwawona, pamene Iye akutengedwera mmwamba. Chotero, mu Chisindikizo cha Chisanu ndi chiwiri momwemo, mukutsanulidwa Mbale, ndipo zina zonse zikutsanulidwa. Chomwe izo ziri, ine sindikudziwa.

115 Zindikirani. Koma tsopano, pa ichi apa, ife tikupeza kuti munthu uyu apa ndi mphungu, munthu uyu amene...kapena Cholengedwa chamoyo ichi chimene chatsanulira apa tsopano. Kapena, mwa kulankhula kwina, pali mibadwo inayi yosiya na ya Izo. Kunali m’badwo wa mkango. Ndipo, Ife tikupeza, uwu kukhala m’badwo wachinai.

116 Ndipo iye anati, “Bwera ndipo udzawone chinsinsi chachinai cha Bukhu la Chiwombolo, chimene chakhala chitabisika mu Bukhu ili. Bwera, udzawone.” Ndipo Yohane anapita kukawona, ndipo iye anawona kavalo wotumbululuka. Ndipo, aponso, wokwera yemweyo pa kavalo wotumbululuka uyu.

117 Tsopano iye ali nalo Dzina lotchedwa Imfa. Tsopano zindikirani. Palibe wa okwera enawo, palibe wa akavalo enawo, kapena palibe nthawi yomwe wokwera uyu anakwerapo, iwo analibe; munthu ameneyo analibe dzina. Koma tsopano iye akutchedwa Imfa. Ilo silikutchulidwa. Mukuwona? Iye akuwululidwa tsopano. Chimene iye ali ali imfa.

118 Chabwino, momwe ife tingachedwere pa icho kwa ulaliki, ndi kuchipangitsa icho kumveka kwenikweni! Koma chirichonse chimene chiri anti, ndicho chotsutsa chenicheni, chiyenera kukhala imfa. Chifukwa, apo pali mitu iwiri yokha, ndiyo, Moyo ndi imfa. Ndipo izo zikutsimikizira kuti vumbulutso la Mzimu Woyera la izi, mu tsiku ili, liri Chowonadi chimodzimidzi. Wotsutsa, iye ali imfa. Chifukwa, Mawu, monga ife titawonere patsogolo apa, ali Moyo. Mukuwona?

119 Ndipo munthu uyu akutchedwa Imfa. Tsopano, ilo silinatchulidwe mu nthawi zina, za wokwera uyu. Koma, pakuti, tsopano ilo likutchulidwa, kuti iye akutchedwa Imfa.

120 Koma pansi pa vumbulutso la mkango...Tsopano yang’anani. Tsopano ine ndikufuna kuwerenga izi mwatcheru, kotero ine ndikhale wotsimikiza; ndinalemba apa, malo, yima apa. Pansi, osati pansi pa vumbulutso la m’badwo wa mkango, kapena la m’badwo woyamba, m’badwo woyambirira, Ili linali lisanawululidwe. M’badwo wotsatira unali m’badwo wa

ng'ombe, umene uli m'badwo wa mdima, m'badwo wapakati, ilo silinawululidwe monga chimene Ilo linali. Ngakhale Chamoyo chonga munthu, cha nzeru, kuyimirira okonzanso, Lutera ndi Wesile ndi ena otero, Ilo linali lisanawululidwe. Koma mu m'badwo wa mphungu, m'badwo wotsiriza, m'badwo wa uneneri, mmene umo muyenera kuwuka kulankhula kwauneneri, mwawona, kwa amene zinsinsi nthawizonse zimafikira! Tsopano apo pali pamene ife chabe. . .

¹²¹ Ife tikhala pamenepo kanthawi pang'ono, usiku uno, kotero kuti inu mumvetsa bwinobwino. Tsopano, mu nthawi zambiri, inu mukuzindikira, izi. . . Ine sindikulankhula chabe kwa gulu ili apa. Matepi awa amapita kulikonse, onani, ndipo ine ndiyenera kupanga izo momveka. Chifukwa, winawake adzatenga tepi imodzi yokha, ndiyeno, ngati iwo satenga ena onsewo, iwo onse adzakhala mmalere, mwawona. Mulungu walonjeza Izi, mwaona, kwa tsiku lino, kwa wotsiriza, kutsirizitsa kwa zinthu zonse zosiyana izi zimene zapitirira ndipo zakhala zitasakanizidwa. Ife tiri. . .

¹²² Ife takhala nazo zovala za Eliya. Ife takhala nayo miinjira ya Eliya. O, pakhala pali anthu amene. . . John Alexander Dowie amene anayikidwa kumeneko, atakulungidwa mu mwinjira. Iye ankati iye anali Elisha. Ndipo ife takhala nayo mitundu yonse ya zinthu monga zimenezo. Nchiyani chimenecho, chonchobe? Ndicho chongoti chichotse Chowonadi chimene chiti chidzaperekedwe. Mwawona? Iwo anali nawo a khristu abodza isanafike nthawi ya Yesu. Mwawona? Iwo nthawizonse amachita izo. Ndi Satana, kuthamanga ndi chokopera, kuti akasokoneze malingaliro ndi chikhulupiriro cha anthu, chinthu makamaka chisanachitike. Ndizo zonse.

¹²³ Kodi Gamalielo sananene chinthu chomwecho kwa Ayuda tsiku lija? Anati, "Kodi panalibe munthu anawuka amene ankadzinerera kuti ali Ichi? Ndipo iwo anatenga mazana anayi kupita mu chipululu. Iwo anawonongeka, ndi zina zotero."

¹²⁴ Anati, "Nthambi iliyonse imene Atate Anga Akumwamba sanayibzale," Yesu anati, "idzazulidwa."

¹²⁵ Gamalielo anati, "Asiyeni iwo okha. Ngati iwo, ngati icho sichikhala cha Mulungu, kodi icho sichidzafika posakhala kanthu? Koma ngati icho chikhala cha Mulungu, inu mudzapezeka mukumenyana naye Mulungu." Munthuyo anagwiritsa ntchito nzeru. Iye anali mphunzitsi.

¹²⁶ Tsopano zindikirani. Tsopano, kuti titsirizitse zinsinsi zonse izi, Mulungu walonjeza kuti pazawuka Elisha weniweni, munthu wina wodzozedwa nawo Mzimu umenewo, ndipo izo zikanadzawululidwa. Iye analonjeza izo mu Malaki 4. Ndipo ine ndiri nazo zolembe ndi makalata zomwe zimanena kuti izo siziri choncho, koma ine ndikanafuna kulankhula naye munthu ameneyo. Mwawona? Bwanji, inu simungachikane icho.

Aliyense weniweni, wazaumulungu wabwino amadziwa izo kuti ziri Chowonadi, kuti iwo akuyembekezera icho.

¹²⁷ Koma kungokhala mwanjira yomweyo monga icho chinabwerera ndi Yohane, wotsogolera wa nthawi yoyamba wa Khristu. Bwanji, iwo sanamuzindikire iye, chifukwa apo panali zinthu zazikulu zotero zitaloseredwera za iye. Bwanji, iye anali “woti apange malo onse okwera kukhala otsika, ndi malo onse otsika kukwera, malo onse oyipa kuwasaladza.” Ndipo, o, iye . . . Aneneri: Yesaya, zaka mazana asanu ndi awiri mphambu khumi ndi ziwiri kusanachitike kubadwa kwake; ndipo Malaki, zaka mazana anai asanabwere iye powonekera; onse awo analosera za iye. Ndipo iwo anali kuyembekezera kakhonde kena ka Kumwamba kuti katsitsidwe, ndipo mneneri uyu atuluke ndi ndodo yake mu dzanja lake, kuchokera kwa Mulungu.

¹²⁸ Ndipo chinachitika nchiyani? Munthu amene inu . . . sakanakhoza ngakhale kuwonetsa khadi lachiyanjano. Iye sakanakhoza kuwonetsa nyota. Ankakhala kutali mu chipululu; wopanda ngakhale maphunziro wamba a sukulu. Iye tawuzidwa, ndi azambiriyakale, kuti iye anapita kuchipululu pamene iye anali zaka zisanu ndi zinayi zakubadwa, itachitika imfa ya abambo ake ndi amayi. Ndipo analeledwa . . . Ntchito yake inali yofunikira kwambiri, kuti ayisokoneze ndi seminare yina. Iye anali—iye ankayenera kulengeza Mesiya.

¹²⁹ Mulungu sakanakhoza kugwiritsa ntchito munthu wokhuta kwathunthu ndi maphunziro azaumulungu. Iye sangakhoze kuchita izo, chifukwa iye nthawizonse azibwerera mmbuyo momwe. Ndiwo mzere wake wa kuphunzirira. Iye amabwerera mmbuyo kwa izo. Kotero, iye azipita nawona chinachake, iye ayesera kubwerera mmbuyo kwa zomwe aphunzitsi anali atanena. Zingakhale bwino ngati inu mutakhala kutali kwa zinthu zimenezo, ndi kungokhulupirira Mulungu.

¹³⁰ Ndipo ife tikupeza kuti iwo anamuphonya iye. Ngakhale atumwi atayima pamenepo, anamuphonya iye. Bwanji, iwo anati, “Bwanji Lemba limati, alembi, amanena kuti Eliya . . .”

¹³¹ Iye anati, “Chabwino, iye wabwera kale, ndipo inu simunamdziwe iye.”

¹³² Ndipo ndi pamene ine ndikufanizira chiwukitsiro, kapena Mkwatulo. Iwo udzapita, ndipo iwo adza . . . ine ndikudziwa izo zikumveka mwachirendo. Koma mwinamwake inu mudziwa mopitirira pang’ono ukapita usiku uno, ngati Ambuye alola, basi momwe ziti zidzakhaliwe, mwawona. Iwo udzakhala mwachinsinsi kwambiri, palibe amene ati adzadziwe za iwo, nkomwe. Dziko lidzangoganiza, kumangopitirirabe monga ilo nthawizonse limachitira, onani, ndipo basi . . . Ndimomwe iye nthawizonse amachitira izo.

¹³³ Inu mukudziwa, ine ndikukayikira ngati mmodzi—mmodzi . . . ine ndikuti, gawo limodzi la makumi asanu ndi

anayi pa zana la anthu pa dziko lapansi, anadziwa konse kuti Yesu Khristu anali pano pamene Iye anali pano. Inu mukudziwa, pamene Eliya ananenera, ine ndikukayika ngati panali konse aliyense amene anadziwa kuti iye analipo. . . Iwo ankadziwa kuti panali chidempete kuntunda uko, wina wakale wotentheka, koma iwo ankamuda iye. Ndithudi. Iye anali chimene iwo ankachitcha wosamvetseka.

¹³⁴ Ndipo ine ndikuganiza, Mkhristu aliyense wobadwa kachiwiri ali ngati wosamvetseka, kwa—kwa dziko, chifukwa iwe wasinthidwa. Ndiwe wochokera ku dziko lina. Mzimu wako uli wochokera kutsidya kwa phompho. Ndipo chinthu ichi apa chiri chosokonezedwa chotero. . . Ndiye, iwe uli—iwe suli wosiyana, pali chinachake cholakwika; iwe, iwe ukadali womangika kwambiri kwa dziko lapansi. Iwe uyenera kukhala wamalingaliro a Kumwamba. Ndipo Kumwamba kumakhaliidwa moyo mwa Mawu.

¹³⁵ Tsopano, ife tikuzindikira kuti ichi—chinthu chachikulu ichi chinachitika. Tsopano, ife tikukhulupirira kuti padzayenera kukhala kubwera kwa Mzimu wowona wa Elisha. Iwo unanenedweratu kuti iwo udzakhhalapo, mwawona. Ndipo ife tiyenera kukumbukira iwo udzakhala pano, mu nyengo yake yomwe ndi nthawi. Ife tikhoza kukhala tikuyika maziko a iwo tsopano. Ndipo iwo sudzakhala bungwe ayi.

¹³⁶ Ine—ine sindikugwirizana naye mzanga wabwino, pa izo. Iye akuti iwo adzakhala gulu la anthu. Ine ndikufuna inu mundiwonetse ine izo mwa Lemba. Mulungu, Mulungu wosasintha, sasintha konse madongosolo Ake. Ngati Iye atero, ndiye Iye sali Mulungu; uko nkulondola, chifukwa Iye ali wachivundi, ndipo Iye amadziwa monga momwe ine ndimachitira, ndipo Iye amalakwitsa.

¹³⁷ Mulungu sanasinthepeo dongosolo Lake, kuyambira nthawi yomwe ya mu munda wa Edeni. Iye anapanga dongosolo la chiwombolo; limenelo linali Magazi. Ndipo ife tayasera maphunziro. Ife tayasera utsogoleri wankhanza. Ife tayasera kuwerenga maganizo. Ife tayasera zazipembedzo. Ife tayasera chirichonse, kukankha aliyense limodzi, kapena kumukonda aliyense limodzi, ndi china chirichonse. Palibe malo ena achiyanjano koma pansu pa Magazi, basi, malo okhawa amene Mulungu amakumana naye munthu.

¹³⁸ Mulungu nthawizonse amachita naye mmodzi payekha. Anthu awiri ali nawo malingaliro awiri. Sipanakhalepo aneneri akulu awiri pa dziko lapansi, akunenera nthawi yomweyo. Yang'anani mmbuyo ndipo muwone ngati analipo. Ayi, bwana. Kuchuluka kusokonezeka kwambiri! Iye ayenera kutenga mwamuna mmodzi wodzipereka kwathunthu, ndi kumugwiritsa nthito munthu ameneyo. Iye amamufunafuna munthu ameneyo.

139 Koma padzakhala mmodzi, nthawi yina, winawake amene ati adzamvere kwa Iye, Mawu ndi Mawu. Ine sindikusamala chimene wina aliyense akunena, iwo sadzasuntha kwa Iwo. Uko nkulondola. Iwo adzayembekezera pa PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo, ndiye, iwo sadzasuntha mpaka nthawiyo. Iye adzatsimikiziridwa mwa bwinobwino. Inu mudza . . .

140 Tsopano, dziko lakunja lidzadana nacho icho, koma Mbewu yosankhidwa, Mbewu yokonzedweratu, monga inalipo mu masiku a Yesu, pamene Kuwala uko kuwalira, Mbewu imeneyo idzabwera ku Moyo monga *chonchi*. [M'bale Branham akhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.] Iwo adzadziwa Izo. Iwo adzamvetsa Izo. Inu simudzasowa kulankhula liwu za Izo.

141 Iye anati, “Bwana, ine ndikuwona kuti Inu muli mneneri. Ine ndikudziwa pamene Mesiya abwera, Iye akuyenera . . .”

Iye anati, “Ine ndine Iye.”

142 Mnyamata, izo, izo zinali zokwanira. Iye sanasowe kuyembekezera usiku wonse, ndi kuyembekezera usiku wotsatira. Iye anali nayo Iyo pomwepo. Iye anali panjira yake. Iye anali kuwawuza iwo za Izo.

143 Tsopano kumbukirani, tsopano, mu m’badwo woyamba unali m’badwo wa mkango. Uwo unali Mkango wa fuko la Yuda, Khristu. Chikopa Chake Chomwe cha Moyo, chinatenga m’badwo umenewo. Ndicho *Chamoyo* choyamba, chimene chimatanthawuza “Mphamvu,” imene inayankha mwa liwu la munthu.

144 M’badwo wotsatira unali m’badwo wa ng’ombe, kapena m’badwo wa wokwera pakavalo wakuda. Mukuwona?

145 Tsopano, chifukwa chimene m’badwo woyamba uwo unali m’badwo woyera, chinali chakuti . . . Monga—monga ine ndakhala nthawizonse ndikumvera anthu akunena kuti wokwera woyamba uyo, woyera, anali mphamvu ya mpingo, unapita kukagonjetsa. Ndipo ife tinapeza kuti iye anapatsidwa korona, kuti uyo anali ameneyo. Iwo unali mpingo. Iwo unali mpingo, koma iwo unapita kuti? Unapita ku Roma. Ndiko kumene iye anachita. Iye analandira korona wake.

146 Tsopano, m’badwo wachiwiri unali u—unali wokwera pa kavalo wofiira, umene unali m’badwo wa mdima.

147 Ndipo tsopano—tsopano, m—m’badwo wotsatira, unali m—munthu, wa m’badwo umene unali wokwera pakavalo wakuda. Ndipo iye anali m’badwo wa okonzanso, onani, pamene l—Liwu limene linalankhula. Tsopano, wokwera pakavalo wakuda, ameneyo anali wotsutsakhristu. Koma Mmodzi amene anali kulankhula mu m’badwo umenewo ankayimiridwa ngati munthu, ndipo ndizo nzeru, kuphunzira, kuthyathyalika. Mwawona? Ndipo iwo sanazimvetse izo, mwawona. Iwo

sanamutche...Iwo sanamutche iye dzina. Mukuwona? Iwo anangoti iye anapita.

148 Koma tsopano, pamene ukubwera m'badwo wa mphungu, ndiwo umodzi umene...Mulungu nthawizonse amafanizira aneneri Ake kwa mphungu. Iye amadzitcha Yekha mphungu. Mphungu imapita mmwamba kwambiri, palibe china chirichonse chingamukhudze iye. Sikuti iye ali kokha mmwamba umo, koma iye anamangidwira malo amenewo. Pamene iye afika mmwamba umo, iye akhoza kuwona pamene iye ali. Anthu ena amafika mmwamba umo ndipo sakhoza kupenya pamene iwo ali, kotero sizimapanga ubwino uliwonse kufika mmwamba umo. Koma ngati inu...

149 Koma inu mumulole khwangwala ayese kuwuluka ndi mphungu, kapena chiwombankhanga, chimodzi chirichonse, iye akhoza kufooka. Iye ayenera kukhala ndi mpweya wa kumene iye akupita.

150 Ndilo vuto lero, ena a ife sitimakhala ndi mpweya. Ife timaphulika msanga kwambiri, inu mukuwona, pamene ife tikulumpha. Ndipo, koma, ife tiyenera kukhala ndi mpweya.

151 Pamene iwe ufika mmwamba umo, ndipo uli nako kupenya kwakuthwa kwa mphungu, kuti uwone zomwe zikubwera, ndi kudziwa choti uchite. Tsopano, m'badwo wa mphungu unawulula Ilo. Tsopano ife tikupeza, kuti m'badwo wa mphungu unalonjezedwa mu Chivumbulutso 10:7 ndi mu Malaki...:1,4. Kuti zikanadzakhala mu masiku otsiriza, mwawona, uko nkulondola, kuti izo zikanadzakhala pano. Chabwino. Zindikirani.

152 Tsopano, munthu uyu, ife tikupeza kuti iye akukwera pa kavalo wotumbululuka. Wotumbululuka! O, mai! Atha, zindikirani atha...

153 "Aprotestanti mamilioni makumi asanu ndi imodzi mphambu asanu ndi zitatu," monga ife tinatenga kuchokera—kuchokera mu *Glorious Reform* la Schmucker, la m—la mbiriyakale ya ofera a Roma, usiku watha. Ife tinapeza kuti, mpaka ku chikhomo cha 1500, ine ndikukhuluprira izo zinali, kapena eyitini-...ine sindikukumbukira bwinobwino tsopano. Koma anali mamilioni makumi asanu ndi imodzi mphambu asanu ndi zitatu anayikidwa ku imfa, kuti atsutse mpingo woyamba wa Chiroma, Roma. Nzosadabwitsa, iye anakhoza kudzizimbayitsa yekha mu dzina losakhala laumunthu la... ndi katchedwa Imfa. Iye ndithudi anali.

154 Tsopano, Mulungu yekha amadziwa kuchuluka kwake amene iye anawapangitsa kufa mwauzimu, mwa kutsutsa-Baibulo kwake, -kuphunzitsa kwa Mawu! Uyu ali iye amene anawayika mamilioni makumi asanu ndi imodzi mphambu asanu ndi zitatu ku lupanga, ndi kuwapha iwo. Ndipo mwinamwake, kwenikweni, mabilioni anafa mwauzimu, pa

kuphonzitsa kwake kwabodza. Nzosadabwitsa iye anakhoza kutenga dzina la Imfa!

¹⁵⁵ Mukumuwona wokwerayo? Pamalo oyamba, monga wotsutsakhristu, iye anali imfa, kuyamba ndi kuyamba; koma iye anali wosalakwa pamenepo. Ndiye iye analandira korona, mmodzi wapatatu; ndipo pamene iye anatero, ndiye iye anayanjanitsa, Satana anayanjanitsa mpingo wake ndi dziko, chifukwa iye anali pamwamba pa zonse izo pamenepo. Wotsutsakhristu anali Satana, mwa mawonekedwe a munthu.

¹⁵⁶ Ndiyeno, komanso, Mateyu Woyera, ine ndikukhulupirira ali, mutu wa 4, akutiwuzwa ife kuti—kuti. Satana anamutengera Yesu, Ambuye wathu, pamwamba, ndi kumuwonetsa Iye mawufumu adziko, onse a iwo, mu kamphindi ka nthawi, ndi ulemerero wa iwo, anawapereka iwo kwa Iye. Ndipo iye anati . . . Iwo, iwo anali ake.

¹⁵⁷ Kotero, inu mukuwona, ndiye, ngati iye angakhoze kuyanjanitsa dziko lake ndi mpingo wake palimodzi, ndiye wokwera pakavalo wofiira akanakhoza kukwera, motsimikiza ndithu. Mukuwona? Mowona! Tsopano, ndiye, ife tikupeza chinsinsi chake apa, mu mpingo wake ndi dziko.

¹⁵⁸ Siteji yachinai ya utumiki wake, iye akutchedwa chirombo. Poyamba iye akutchedwa wotsutsakhristu, onani; ndiye iye akutchedwa mneneri wabodza; ndipo iye akutchedwa chirombo. Tsopano ife tikumupeza iye apa akutchedwa monga chirombo. Tsopano, ine ndikufuna inu muzindikire, ndizo potsatira kavalo wachinai.

¹⁵⁹ Ndipo mu kavalo wachinai uyu, ngati inu muti muzindikire, zonse . . . Mmodzi woyamba anali woyera; ndiyeno mmodzi wotsatira anali wofiira; ndipo mmodzi wotsatira anali wakuda; ndipo mmodzi wachinai, onse a awa ena atatu anayimiridwa mmenemo; chifukwa, kutumbululuka kuli kufiira ndi—ndi kuyera, ndipo kotero, kutasakanizidwa pamodzi. Mwawona? Iye . . . Izo—izo zonse zinasakanizidwa mu kavalo mmodzi uyu. Mwawona? Ndipo pamenepo iye akukhala anai, kapena, makamaka, atatu mwa mmodzi. Ndipo zinali zonse zitasakanizika mu chinthu chimodzi icho.

¹⁶⁰ Tsopano ine ndikufuna inu muzindikire anai a iwo. Zindikirani kuphonya-malo, kwa zinai, kwa masamu auzimu. Mulungu ndi zitatu. Izi ndi zinai. Iye ali mu unai, apa. Poyamba, wotsutsakhristu, woyera; kachiwiri, mneneri wabodza, wofiira; kachitatu, vaikara wa miyamba ndi dziko lapansi ndi—ndi purigatorio, wakuda; kachinai, chirombo, kavalo wotumbululuka, Satana kukhala atakankhidwa kuchokera Kumwamba. Kodi inu mukufuna kuwerenga zimenezo? Chivumbulutso 12:13, Satana kukhala atakankhidwa kuchokera Kumwamba. Ndiye mu Chivumbulutso 13:1,8, iye ali mu thupi mwa munthu wa chirombo.

¹⁶¹ Iye ali poyamba wotsutsakhristu, basi—chiphunzitso chabe chotchedwa Chinikolai; ndiye iye akukhala, kuchokera kwa icho, kukhala mneneri wabodza. Ngati iye ali wotsutsakhristu, wotsutsakhristu ali *wokana*. Chirichonse chimene chiri chotsutsa Mawu a Mulungu chiri chotsutsa Mulungu, chifukwa Mawu ali Mulungu. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anasandulika thupi, Khristu, ndipo anakhala pakati pathu.” Ndipo tsopano iye akutsutsa Mawu, kotero iye akukhala wotsutsakhristu. Koma mzimu sungavekedwe korona; ndicho chifukwa chake iye sanalandire korona. Uta chabe, wopanda mivi.

¹⁶² Ndiyeno pamene iye anafika, nthawi yovekedwa korona, ndiye iye akukhala mneneri wabodza wa chiphunzitso chake chotsutsakhristu. Mwamva izo? Ndiye iye akutenga lupanga, chifukwa iye akuyanjanitsa mphamvu zake palimodzi, ndiye iye sayeneranso kufunsa aliyense. Iye ali kazembe wa dziko; iye ali kazembe wa Kumwamba. Akulandira korona wa patatu. Iye akudzipangira yekha ganizo lotchedwa “purigatorio.” Kumene, ngati—ngati ena a iwo anamwalira mmbuyo umo, ndipo iwo ali nazo ndalama zina, akufuna kulipira kuti achokeko, iye akhoza kuwapempherera iwo kuti atuluke kumeneko. Chifukwa, iye ali nayo mphamvu yochitira zimenezo; iye ali *vikara*. Ndithudi, iye ali. “Iye akutenga malo a Mulungu, padziko lapansi.” Ngati izo siziri zomveka monga chirichonse!

¹⁶³ Ife tikuzipeza izo, kukokera izi pansi, mu Baibulo lonse, ndi kuwerenga nambala mawerengero ake ndi china chirichonse. Apa iye ali. . . ? . . . mmbuyo momwe umu mu nambala yachinayi, osati nambala yachitatu. Nambala yachinayi, mwawona.

¹⁶⁴ Tsopano tiyeni titsegule, Chivumbulutso 12. Tiyeni tiwerenge chabe izi pang’ono pokha, chifukwa ife—ife tikhala nayo nthawi yochitira izo. Ndipo tiyeni tiwerenge Chivumbulutso m—mutu wa 12 ndi ndime ya 13. “Ndipo ora lomwero kunali chivomezi chachikulu. . .” Ayi, ine ndapeza—ine ndapeza malo olakwika. Ya 13:

Ndipo pamene chinjoka chinawona kuti iye anaponyedwa ku dziko lapansi, iye anazunza mkazi amene anabala mwana wamwamuna.

¹⁶⁵ Tsopano, inu mukuwona, iye anaponyedwa kunjwa, pa dziko lapansi, ndi kukhala mu thupi, monga mzimu wotsutsakhristu ukukhala mu thupi mwa munthu. Munthu ameneyo akusinthwa kuchoka ku chinthu chimodzi kupita ku china, kuchoka ku mzimu wotsutsakhristu kukhala mneneri wabodza, ndiyeno chirombo chikubwera mwa iye.

¹⁶⁶ Chimodzimidzi basi monga Mpingo umakulira; mpingo wake unadutsa kuchokera—kuchokera kwa wotsutsakhristu kwa mneneri wabodza, ndipo, mu m’badwo wopambana wakudza, chirombo chimene chiti chidzawuke. Kotero, Mpingo

ukubwera mwa njira yomweyo, kupyola mu kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, uli Khristu kukhala mwa anthu, chimodzimodzi basi. Ndipo iye ali nacho chotsutsana cha Ichu pamwamba apa, . . . onani, choyimira cha Ichu, kani. Apo iye ali, chimodzimodzi basi. Ndiye iye. Iye wakankhidwa kuchokera Kumwamba.

167 Tsopano ife tikupeza, mu Chivumbulutso 13:1 mpaka 8.

Ndipo ine ndinayimirira pa michenga ya mnyanja, ndipo ndinawona chirombo chikuwuka. . .

168 Tsopano, apa pali 12, pamene iye anakankhidwira kunjira. Tsopano yang'anani.

. . . ndinawona chirombo chirinkutuluka kuchokera mnyanja, chiri nayo mitu isanu ndi iwiri ndi nyanga khumi, ndipo pa nyanga zake nduwira khumi, ndi pa mutu wake dzina la mwano.

Ndipo chirombo chimene ine ndinachiwona chinali chonga nyalugwe, ndipo mapazi ake. . .

169 O, ngati ife tikanangokhala nayo nthawi tsopano, ife tikadatenga usiku wonse, pa zophiphiritsa zimenezo zomwe pamenepo, ndi kuwonetsa, kuzibweretsa izo molunjika kwa iye kachiwiri. China, pafupi ambiri ainu nonse mukudziwa izo, kuchokera ku maphunziro ena.

. . . anali. . . mapazi chimbalangondo, ndi pakamwa pake. . . pakamwa pa mkango: ndipo chinjoka chinamupatsa iye mphamvu, . . . mpando, ndi. . . ulamuliro.

170 A! Satana mthupi! Mwawona?

Ndipo ine ndinawona umodzi wa mitu yake ngati iwo. . . unavulazidwa kwa imfa; . . .

171 Ndipo mpaka mmusi, pamene ife tikupitirira, ngati inu mukufuna kutero, pamene inu mukapeza mwayi wowerenga mpaka mmusi. Ayi, tiyeni—tiyeni tingowerenga pang'ono pokha.

Ndipo ine ndinawona umodzi wa mitu yake monga ngati iwo unavulazidwa. . . imfa; ndipo bala lake la ku imfa linapola: ndipo dziko lonse linazizwa potsata chirombo.

172 Inu mungoyang'ana! Inu musati konse muyang'ane chikominisi. Ichu sikanthu koma chida, chikusewera mmanja a Mulungu, kuti chidzakuthandizeni inu tsiku lina kupeza, “kubwezera magazi,” monga mmene ife titi tidzapeze usiku wa mawa. Mwawona?

Ndipo iwo anapembedza chinjoka. . .

173 Anali chinjoka ndi ndani? Satana. Uko nkulondola? “Chinjoka chofiira.” Chabwino.

...chimene chinapereka mphamvu kwa chirombo (kumene iye akutenga mphamvu yake, mwawona): ndipo iwo anachipembedza chirombo, kunena, Ndani ali wofanana nacho chirombo? ndani akhoza kupanga nk'hondo naye iye?

Ndipo kunapatsidwa kwa icho kamwa yolankhula zinthu zazikulu za mwano; ndipo mphamvu inapatsidwa kwa iye kukapitiriza miyezi makumi anai ndi iwiri.

Ndipo iye anatsogola kamwa yake mwa mwano motsutsa Mulungu, (Ndi zimenezotu, mwawona. Chabwino)...kuchitira mwano dzina lake, (kumupatsa iye udindo)...kachisi wake (amene ali malo okhalapo Mzimu Woyera),...

174 Kuwapanga iwo malo mu Roma, Mzinda wa Vatikani. Inu mukhoza kumangopitirira mpaka mmusi:

...ndi iwo akukhala mmwamba.

175 Anawachitira mwano iwo, pakunena kuti iwo anali otezerera.

Ndipo kunapatsidwa kwa iye kupanga nk'hondo nawo oyera (ndipo iye anachita), ndi kuwagonjetsa iwo (iye anachita)...

176 Kuwawotcha iwo pa nk'huni! Kuwadyetsa iwo kwa mikango! Ndi kuwapha iwo mwa njira iliyonse iye akanakhoza!

...ndipo mphamvu inapatsidwa kwa iye pa mitundu yonse, ...malirime, ndi mafuko.

177 Izo sizinafike chotero mu Roma mpaka Roma wachikunja atatembenezidwa kukhala Roma wa upapa, ndipo mphamvu ya Chikatolika inafalikira pa dziko, anapanga mpingo wa Chikatolika wa konsekonse.

Ndipo onse amene akukhala pa dziko lapansi adzamupembedza iye, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu...

178 "Usakhudze Mafuta Anga ndi vinyo!" Mwawona?

Ndipo onse amene akhala pa dziko lapansi adzamupembedza iye, amene maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo wa Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko.

Ngati munthu aliyense ali nalo khutu, mloleni iye amve.

Iye amene atsogolera ku ndende adzamuka ku ndende: iye amene apha ndi lupanga ayenera kuphedwa nalo lupanga. Apa pali chipiriro ndi... chikhulupiriro cha oyera.

179 Tsopano, ife tinali naye iye akubwera, usiku watha, ndi lupanga lake lalikulu, kukapha.

180 Ife tikupeza kuti iye akuphedwa nalo lupanga, nayenso, lupanga la Mawu. Mawu a Mulungu, akuthwa, lupanga lakuthwa mbali ziwiri, kumudula iye, kumusiya iye pansu pomwe. Yembekezani mpaka Mabingu Asanu ndi awiri awo atalankhula maliwu Awo, a gulu ilo amene angakhoze kutenga kwenikweni Mawu a Mulungu ndi kuwapereka Iwo uko, Iwo adzayengula ndi kudula. Ndipo iwo akhoza kutseka miyamba. Iwo akhoza kutseka *ichi*, kapena kuchita *icho*, chirichonse chimene iwo akufuna kuteru. Ulemerero! Iye adzadulidwa nawo Mawu amene akutuluka kuchokera mkamwa Mwake, ali akuthwa kuposa lupanga lakuthwa mbali ziwiri. Iwo akhoza kuyitana matani mabilioni zana a ntchentche ngati iwo angafune kuteru. Amen. Chirichonse chimene iwo anena, chichitika, chifukwa Ndiwo Mawu a Mulungu akubwera kuchokera mkamwa mwa Mulungu. Eya. Amen. Mulungu, nthawizonse, Ndiwo Mawu a Ake, koma Iye nthawizonse amagwiritsa ntchito munthu kuchita Zimenezu.

181 Mulungu akanakhoza kuyitana ntchentche zija, kuja ku Igupto, koma Iye anati, “Mose, ndiyo ntchito yako. Ine ndikuwuzwa chabe iwe choti uchite, ndipo iwe upite ukachichite icho.” Iye anachita icho mokwanira. Mwawona? Iye—Iye akanakhoza kusankha—dzuwa kuti liyitane izo, Iye akanakhoza kupangitsa mwezi kuti uyitane izo, kapena mphepo kuti iyitane izo. Koma, Iye—Iye anati, “Mose.” Kuti, kuti. . . Iye anasankha munthu Wake. Chabwino.

182 Tsopano ife tinapeza apa, kuti Satana uyu, atatha kukankhidwa Kumwamba, akudzikhazika yekha mu thupi mwa chirombo. Ndipo tsopano iye ali chirombo; wotsutsakhristu, mneneri wabodza, ndipo tsopano chirombo. Ndi kupatsidwa dzina la Imfa! Ndipo Gehena ikumutsata iye! Satana wathunthu, pa mpandowachifumu wake! O, mai! Pa dziko lapansi, iye ali Satana, woyimira, pa dziko lapansi, kuti iye tsopano ali mutu wa maufumu a dziko, maufumu omwewo amene iye anawapereka kwa Ambuye Yesu mu Mateyu 4. Satana tsopano akukhala mfumu yathunthu.

183 Tsopano, izi zikuchitika kenako. Iye ali mneneri wabodza tsopano. Iye adzakhala chirombo, pakapita kanthawi, pamene iye aswa pangano lake kumeneko ndi Ayuda. Inu mukudziwa momwe ife. . . Chabwino, zindikirani tsopano, iye adzapatsidwa mtima wa chirombo, pa nthawi imeneyo, ndipo Satana adzadziziyika yekha mu thupi. Chifukwa, pamene Mpingo ukupita mmwamba, Satana akuponyedwa kunja. Mukuwona? Mukuwona? Izo zatheka, ndiye, kutsutsa kwake konse kwatha. Mukuwona? Tsopano, malingana ngati. . .

184 Taonani, malingana ngati Wotetezera akadali pa Mpandowachifumu, Satana akhoza kuyima pamenepo ndi kutsutsa, chifukwa iye ali woyimira mulandu wa mbali inayo. Iye ali mdani wa Khristu. Ndipo Khristu ali... Iye akuyimirira pamenepo, m—m—mdani akuyimirira pamenepo, akuti, “Koma, yembekezani! Adamu anagwa! Adamu anachita *ichi!* Ine ndinamugonjetsa iye. Ine ndinampanga mkazi wake kukhulupirira bodza. Ndipo Inu munati iye akanadzawonongedwa nalo ilo. Ine ndinapeza izo!”

185 Koma apa pali Mkhlapakati atayimirira pamenepo, ameni, Wowombola Wachibale, ameni, atayimirira pamenepo ndi Magazi amene angakhoze kutenga mtima wa wochimwa woyipisitsa ndi kuwusinthwa iwo. Mkhlapakati ali pa Mpandowachifumu. Inde, bwana.

Satana anati, “Koma iwo ali ochimwa!”

Iye akhoza kunena, “Iwo sali ayi.”

186 Cloroxi imeneyo inatulukiridwa, kapena kupangidwa, kuti izitenga banga, kutenga kuthimbiritsa kwa inki kapena banga lina lililonse. Iwo ali nayo iyo. Iyo idzaswa ilo mpaka inu simudzalipeza konse ilo kachiwiri. Ilo limabwerera ku mipweya, ndipo njira yonse kubwerera ku kuwala kwa dziko. Ndi kupitirira ma molekyulu ndi china chirichonse, mpaka ilo litabwerera koyambirira kumene ilo linachokera. Chirengedwe chake. Chinachita... Chirengedwe chinachita kubwera kuchokera kwa Mulengi. Koma mapulusa onse amene anapangidwa ndi kuyikidwa palimodzi, iwo aswedwa, ndipo ndicho basi chomwe chiripo kwa ilo. Palibe zinsano za ilo. Ngakhale limene—thunthu limene la madzi ilo liri, kugwirizana ndi Cloroxi, amene ali maphulusa.

187 Ameni! Ulemerero kwa Mulungu! Zonse ziri zoyera. Ndicho chimene Magazi a Yesu Khristu amachita kwa mwana wowona wa Mulungu, pamene iye alapa tchimo limenelo ndi kuyima pamenepo, wolungamitsidwa mu Chake... Chifundo! Ubwino! Ngakhale liri lalikulu mpaka Mulungu anati, “Ine sindingakhoze ngakhale kulikumbukira ilo nkomwe. Ndipo iye ali mwamtheradi mwana Wangwa.”

188 “Indetu, Ine ndinena kwa inu, ngati inu munena kwa phiri ili ‘sunthidwa,’ ndipo simukukayika mu mtima mwanu, koma mukukhulupirira mu chimene inu mwanena, inu... chidzachtika. Inu mukhoza kukhala nacho icho chimene inu mwanena kuti chikanadzakhala.” Inu ndinu mwana wowomboledwa. Ameni! Ine ndikudziwa izo nzowona.

189 Ine ndawonapo agologolo akuwonekera kutsidyako, pa nthawi zisanu ndi imodzi zosiyana, zomwe ine sindinadziwe mmodzi amene akanakhala apa. Chabe monga, Iye akhoza kulenga agologolo mofanana ndi momwe Iye angakhoze kulengera ntchentche kapena achule, kapena china chirichonse.

Iye, Iye ali Mulungu, Mulengi. Kulondola! Ndipo pamene palibe munthu wachivundi. . .

¹⁹⁰ Koma pamene tchimo ilo la chivundi ilo lalapidwa ndi kugwetseredwa mu Cloroxi iyo, ya bulitchi ya Yesu Khristu, Iyo imachotsa tchimo lonse. Iye ali mwangwiro wosakhudzidwa, wopanda tchimo, wopanda cholakwika. “Iye amene abadwa wa Mulungu samachita tchimo, pakuti iye sangakhoze kuchimwa.” Bulitchi imayima pakati pa iye ndi Mulungu. Lingakhoze bwanji ilo kufika nkomwe pamenepo, pamene iyo iswa ilo ndi kulumiza ilo mmbuyo kumene kwa iye amene anasokoneza ilo! Ameni!

¹⁹¹ Psyi! Ine ndikumverera mwachipembedzo. Ine—ine ndikukuwuzani inu, ine ndikukondowedwa tsopano pamene izi zikuyamba kuwululidwa.

¹⁹² Zindikirani, kwathunthu Satana, pa mpandowachifumu wake. Inde, bwana. Anawupereka iwo kwa Mulungu, anawupereka iwo kwa Ambuye wathu. Apa iye ali, atakhala apa, ndi mtima uwu wa chirombo mwa iye. Tsopano, apa pali munthu, chirombo, Mdierekezi mu thupi. Iye akupanga mawonekedwe ake apa pa dziko lapansi, mwa kunyengezera kwabodza. O, mai, ubwino! Pansi pa kunyengezera kwabodza kwa Mawu owona, iye akudziyanjanitsa yekha nawo Mawu.

¹⁹³ Iye anachita basi chinthu chomwecho chimene wake—woyimira wake anachita, amene anali Yudasi, zaka zikwi ziwiri zapitazo. Anachita chiyani iye? Yudasi analowamo, ngati wokhulupirira, pokhala Mdierekezi kuchokera pachiyambi. “Iye anabadwa mwana wachitayiko.” Iye sanakoke kanthu pa Yesu, chifukwa Iye ankamudziwa iye kuchokera ku chiyambi komwe; ameni, pakuti Iye anali Mawu. Chabwino. Ndipo, kumbukirani, Yudasi anatenga malo monga msungichuma, ndipo anagwa ndi ndalama.

¹⁹⁴ Kotero ukuchita mpingo wa tsiku ili! Mpingo wa Katolika, monga ife tinazindikira usiku watha, ukulipiritsa kudzitunduzwa, kulipiritsa mapemphero, ndi kulipiritsa chirichonse. Ziri pafupi zofanana, ndipo anagwa chinthu chomwecho kwa ana aakazi a mpingo wa Katolika, anali Aprotostanti. Chinthu chonse chakutiridwa mu ndalama. Apo ndi pamene Yudasi anagwera, ndipo apa pali pamene iye anagwera, ndipo apo pali pamene Aprotostanti akugwa.

¹⁹⁵ Yang’anani, akukwera kavalo wotumbululuka pamene iye akuwonekera pa kukwera kwake, kukwera kotsiriza uku. Iye ali pa wotsiriza wake tsopano. Tsopano, izo si mu tsiku lathu. Izo zidzakhala mmusi umo. Ndi Chisindikizo, choloseredwa. Chifukwa, taonani, Mpingo wakwera kale pamene izi zikuchitika. Pamene Khristu akuwonekera apa pa dziko lapansi, pamene—pamene—pamene. . . Munthu uyu akuwonekera, ndipo akukhala kwathunthu, kwathunthu

Mdierekezi; kuchokera kwa wotsutsakhristu, njira yonse mpaka mmusi, kupyola mneneri wabodza, ndiye mpaka mwa chirombo, Mdierekezi mwiniwake. Ndipo iye akukwera pa kavalo wotumbululuka, wamitundumitundu yonse, ndi wosakanizidwa nayo mitundu yosiyana yonse, kuti imupange iye wotumbululuka ndi waimfa.

¹⁹⁶ Koma pamene Ambuye wathu akuwonekera kuno pa dziko lapansi, Iye adzakhala atakwera pa kavalo woyera ngati chipale. Ndipo Iye adzakhala mwathunthu, mokwanira, Emanueli, Mawu a Mulungu mu thupi mwa Munthu. Mukuwona? Ndiko basi kuchuluka kwake kwa kusiyana kulipo mwa iwo. Ndiko kusiyana kwa iwo.

¹⁹⁷ Zindikirani, wotsutsakhristu ali pa kavalo wotumbululuka, wosakanizika mitundu. Kavalo ali chirombo chimene chimayimira mphamvu. Mphamvu yake ili yonse yosakanizika. Chifukwa? Ndizo ndale, ndizo—ndizo mphamvu zafuko, ndizo mphamvu zachipembedzo, ndizo mphamvu za ziwanda. Ndizo mphamvu za mitundu yonse zitasakanizidwa pamodzi, wosakanizika, kavalo wotumbululuka anali. Iye ali nazo mphamvu za mitundu yonse.

¹⁹⁸ Koma pamene Yesu abwera, ali pa kavalo wa mtundu umodzi wolimba, Mawu. Amen!

¹⁹⁹ Mmodzi uyu akusakaniza mitundu yake, wofiira, woyera, wakuda; mitundu itatu mu umodzi, kuyimiridwa mu umodzi. Ndipo mphamvu zitatu kuyimiridwa mu umodzi; kavalo woyera, kavalo wakuda, kavalo wofiira. Ndi akorona atatu, mwa mmodzi. Mwawona? Ndithudi.

²⁰⁰ Ine ndinamuwona korona, mwiniwanga; ndinayima, o, pafupi *chonchi* ndi kuyang'ana pa iyo. Sakadandilola ine kufika pa iyo, pa chifukwa cha galasi, pa iyo. Kotero uyo anali pamenepo, loko wamkulu pa iye, atakhala mu chikwama; korona wapatatu. Kotero ine ndikudziwa ndi chowonadi. A-nha. Kotero apo iye anali, korona wapatatu, vaikara: kumwamba, purigatorio, ndi dziko lapansi.

²⁰¹ Mphamvu zitatu kulumikizana palimodzi, mwawona, zonse kusakanizika mu mtundu, wotumbululuka. Imfa inalankhula mu chinthu chonsecho; ndale, ndi—ndi zipembedzo, ndi—ndi mphamvu ya ziwanda, kusakanizika palimodzi. Ndale, iye ali mfumu ya ndale, Satana ali. Wanzeru! Psyii! Ndithudi. Musati muyesere kumuposa iye. Ingo—ingodalirani Ambuye. Ndizo zonse.

²⁰² Monga ndakhala, tonse, tinapoyolamo izo kale. Onse anzeru, maphunziro ndi zinthu monga choncho, kuchokera ku mbali yolakwika. Ingotsatani izo kupyola mu Lemba, mupeze ngati uko kuli kulondola. Muwatsate ana a Kaini ndipo muwaone chimene iwo anakhala. Ndiye mutsate ana a Seti, onani chimene iwo anali. Osati kuti ndikuthandizira umbuli, ayi konse. Ayi,

bwana. Koma inu mutenge za munthu aliyense, nkomwe, wa Baibulo, nzosachitika kwambiri . . .

203 Ndipo pali mmodzi wotchedwa Paulo, yemwe anali munthu wophunzira, ndipo iye anati iye anachita kuyiwala chirichonse iye ankachidziwa, polinga kuti adziwe Khristu. Iye anati, “Ine sindinabwere kwa inu ndi mawu odolola a nzeru za anthu, koma ine ndabwera kwa inu mu Mphamvu ya chiwukitsiro cha Khristu.” Uko nkulondola, Mphamvu ya Mzimu Woyera!

204 Yang’anani pa ena. Ena a iwo sankadziwa ngakhale kusiyantsa dzanja lamanja ndi la manzere. Ndipo—ndipo, o, yang’anani mmusi kupyola mu m’badwo wa aneneri, ndi kumene iwo ankachokera, ndi zina zotero. Mukuwona chimene ine ndikutanthawuza?

205 Onani, ali ophunzira, aluntha, ndi anzeru. Nzeru ziri chimodzimodzi chinthu chomwecho chimene chimakutengera iwe kutali ndi Mulungu.

206 Iye anali nazo mphamvu zitatu, kapena zitatu—ulamuliro utatu: dziko lapansi, Kumwamba, ndi purigatorio.

207 Iye ali, mwiniwake, utatu. Ndicho chimene iye wapangidwa nacho. Ndipo iye akukwera mu utatu. Mphamvu yake ili mu utatu. Korona wake ali mu utatu. Kavalo wake ali mu utatu. Ndi chimene iye ali, utatu; mphamvu ya utatu, korona wa utatu, kavalo (akukwera) wa utatu; ndiwo maudindo, zinai apanso, onani, zinai apanso. Chabwino.

208 Masiteji atatu a utumiki wake, akumupanga iye munthu mmodzi, Satana mthupi. Masiteji atatu a utum-. . . wotsutsakhristu, mneneri wabodza, ndi chirombo. Zitatu izo, kuyimira, mwawona. Tsopano apo pali zoyimira zitatu, tsopano, apo zikumupanga iye.

209 Mulungu, Mulungu amadzidziwitsa Yekha, nayenso, mu madzi, Magazi, Mzimu; zimamupanga Mkristu mwana wa Mulungu, mwa Mawu a Mulungu. Mukuwona? Ndipo mphamvu *zitatatu* izi zikumupanga iye Mdierekezi. Mukuwona? O, Awa apa, ali madzi, Magazi, ndi Mzimu, zomwe ziri za Mulungu. Ndipo *izo* ndi ndale, chipembedzo ndi mphamvu ya ziwanda, kusakanizika pamodzi, zikumupanga iye Mdierekezi.

210 Kudza koyamba kwa Khristu, wachivundi. Iye akubwera nthawi zitatu. Khristu ali mu patatu. Mukuwona? (Yang’anani momwe iye akubwerera; iye ali panayi.) Muyang’anani Khristu. Kudza koyamba, Iye anabwera wachivundi, kudzakhetsa ndi kufa. Nkulondola uko? Ndiko kudza Kwake koyamba. Kudza kwachiwiri ndiko Mkwatulo; ife tikomana naye Iye mu mlengalenga, wachisavundi. Kubwera Kwake kwachitatu. Iye ali Mulungu mu thupi. Ameni! [M’bale Branham awombetsa manja ake pamodzi kamodzi—Mkonzi.] Mulungu, Emanueli, kudzalamulira pa dziko lapansi! Uko nkulondola, katatu kokha.

211 Siteji yachinai ya wokwera, yang'anani. Siteji yachinai ya wokwera uyu ikutchedwa Imfa. *Imfa* imatanthawuza “kulekana Kwamuyaya ndi Mulungu.” Ndicho chimene imfa imatanthawuza, kukhala olekanitsidwa Kwamuyaya ndi Mulungu.

212 Tsopano, ngati ife tamuyika munthu uyu panja, kalasi, ngati ife tawonetsa mwa Baibulo, yemwe munthu uyo ali; ndipo ife ngakhale tatenga mapiri, malo ndi paliponse, kungokhala chimodzimodzi molongosola, kupitirira mpaka mmusi. Ndipo tsopano iye akutchedwa, ndi mphungu, “Imfa.” Ndicho chimene Iye akumutcha iye. Kumbukirani, apa, onani, imfa ili kulekana Kwamuyaya.

213 Kumbukirani, oyera samafa. Iwo amagona, osati kufa. “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya.” Uko nkulondola. “Sadzafika mu chiweruzo; wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Ine ndine chiwukitsiro ndi Moyo,” anatero Yesu. “Iye amene akhulupirira mwa ine, ngakhale iye anali wakufa, komabe iye adzakhala moyo. Ndipo aliyense amene akhala moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse.” Lazaro, wafa? “Iye akugona.”

214 “Musawope ayi, msungwana sali wakufa, koma akugona.” Iwo anamuseka Iye momunyodola. Nkulondola uko? O, mai! Onani, oyera samafa.

215 Kulekana ndi Mulungu ndiyo imfa, imfa Yamuyaya. Ndipo munthu uyu akutchedwa “Imfa,” kotero khalani kutali ndi iye. Ali ndani iye? Ka bungwe, kachitidwe ka bungwe; woyamba, mpingo wa nambala wani, unachita bungwe, ndipo pamene iye anatenga—kumvetsa kwa Konstantini, ku Khonsolo ya Nicaea.

216 Ife tinawabweretsa akazi amenewo, usiku watha, ndi kuwonetsa momwe Eva, mkwatibwi woyamba, mwamuna wake asanafike konse kwa iye, iye anagwa, pa kusakhulupirira Mawu a Mulungu mu Edeni. Mkwatibwi wauzimu amene anabadwa pa Tsiku la Pentekoste wa Khristu, asanafike Iye kwa mkaziyo, chinachitika nchiyani? Iye anagwa, ku Roma. Chiyani? Anapinyolitsa ukoma wake wa Mawu, kwa miyambi. Amen. O, mai!

217 Ine—ine—ine ndikumverera kukondoweza kukubwera kachiwiri pa ine, inde, bwana, kuganiza za zimenezo. . . Ine sindikutanthawuza kuchita mopenga. Ine sindikutanthawuza zimenezo. Koma ine chabe. . . Inu simukuzindikira chomwe izo zimachita kwa ine. Ine ndakhala ndikukhala pa izi kwa masiku anai tsopano. Chabe. . . ndipo ine ndikungoyenera kulankhula chinachake, kuti chinditengere ine kumverera mwa umunthu kachiwiri. Inu mukudziwa chomwe ine ndikutanthawuza. Eya. Chabwino. Kuyamba kulankhula monga choncho, ndipo iwe umawona masomphenya akufalikira pamaloponse.

Uko nkulondola. Mwawona, ndicho chifukwa chake ine ndikunena chinachake kuti ndizibweze ndekha kachiwiri, ndi kudzigwedezanso kachiwiri. Mukuwona?

218 Kodi inu munayamba mwazindikirapo ine pamene ine ndiri nawo mzere wa kuzindikira za mumtima? Ine ndimanena chinachake, chimene chiti chiwapange anthu kuseka; ndiye ine ndimanena chinachake, chimene chiti chiwapange anthu kulira; ndiye ine chinachake, chowapangitsa iwo kukwiya. Ine ndapeza chinachake chitawonekera. Ndipo ine ndimanena chinachake, kuti ndiwone momwe icho chikutengera, ndiye ine ndimawona mtundu wa kuwala umene uli pa iwo, zimene zikuchitika. Ine ndimadziwa pamene icho chiri, ndipo ine ndimadziwa ngati Iwo ukuyitana kapena ayi. Ngati iwo suli. . . Ukukhala pamenepo, wokhulupirira weniweni, chabwino. Iwe uwayitana iwo, ndiye, kunena, “Inu, *Akuti-ndi-akuti.*”

219 Ndipo pamene iwe ufika mmusi, Mzimu umayamba kudzoza, ndiye umayamba kuwona kuthwanima uko kukubwera paliponse, onani, monga choncho, kuzungulira, kuzungulira mchipinda. Kotero, ndicho chifukwa chake ine ndimanena chinachake, kukhala ngati kuyambira mmbuyo kachiwiri, kuyambiranso mwatsopano kachiwiri, mwawona.

220 Kuyambira Lamlungu latha, ine ndinangokhala mu chipinda, kumangopemphera, ndizo zonse, ndi pansi pa kudzoza. Ndipo ine ndikudziwa Izi nzolondola. Inu mukhulupirire Mulungu. Ine ndikudziwa inu mmatero. Inu mungoyang’ana pa mapeto a sabata. A-nha. Mwawona? Mwawona? Chabwino. Mwawona?

221 Tsopano, imfa imatanthawuza kulekanitsidwa Kwamuyaya ndi Mulungu. Ndipo kumbukirani, tsopano, oyera samafa.

222 Kumbukirani, mkwatibwi wake anapatsidwa kavalo wotumbululuka. . . ine ndikutanthawuza, wokwera uyu anapatsidwa kavalo wotumbululuka, ku—kuti azipita naye. Iye anapatsidwa uyu—kavalo wotumbululuka uyu, kuti azipita naye. Ndipo iye anakwera kavalo wotumbululuka uyu, wa imfa. Tsopano ife tikudziwa chomwe icho chinali. Ife tikudziwa mpingo wake umene unali.

223 Ndipo kumbukirani, mu usiku watha, iye sanali kokha “hule,” iye anali “mayi wa timahule.”

224 Ndipo ife tikupeza, kuti chimene chinamupanga iye hule, chinali, mkazi amene ali mkazi wa mtundu umenewo. Ine ndiri chabe. . . Ndi mawu osabisa, kuwalankhula pakati pa gulu losanganikirana. Koma Baibulo limanena zimenezo, inu mukuwona. Kotero, ndiye, ife tikuzindikira kuti ndiye—ndiye mkazi amene amakhala moyo wosalungama kwa malumbiriro a ukwati wake. Ndipo inu mwawona, iye akuyenera kukhala, akunena yekha, kudziticha yekha, “Mfumukazi ya Kumwamba.” (Ameneyo akanakhala Mkwatibwi wa Mulungu. Mulungu ndi

Khristu.) Ndipo ife tikupeza kuti iye akuchita ziwerewere, ndipo iye akuwapangitsa mafumu a dziko lapansi kuchita ziwerewere, ndi anthu onse olemera, ndi anthu opambana. Dziko lapansi lonse linamutsata iye. Mukuwona?

²²⁵ Ndiyeno ife tikupeza kuti iye anabereka ana aakazi ena, ndipo iwo anali timahule. Kodi kahule ndi chiyani koma hule, chinthu chomwecho; wachiwerewere, ziwerewere, zoyipa, zigololo, kuchita. Kodi iwo anachita chiyani? Anapanga bungwe, anatenga kachitidwe, anaphunzitsa zopangidwa ndi munthu, Pentekoste ndi gulu lonse!

²²⁶ Tsopano, musati mulole chanu—chikumbumtima chanu chigwere mu thumba lanu, Pentekoste. Ndiroleni ine ndikuwuzeni inu chinachake. Tiyeni tiyang'ane chinthucho mu nkhope momwe. Ife tachedwa kwambiri panjirayi tsopano, kuti tizipita tikubweza nkhoonya. Yang'anani apa.

²²⁷ Ife tikukhala mu M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya. Ndipo umenewo unali m'badwo wa mpingo wautsiru kwambiri mwa yonse ya iyo, wofunda, ndipo umodzi wokha umene Khristu anali kunja, kuyesera kuti abwere mkati. Ndipo ndiwo uthenga Wachipentekoste ukupita, anati, “Ndine wolemera!” Mnyamata, iwe unali wosawuka, poyamba. Tsopano iwe wakhaladi wolemera, mwawona. “Sindisowa kanthu!” Ndipo—ndipo, o, chimene iwe unali!

²²⁸ Iye anati, “Ndiwe wamaliseche, wochititsa chifundo, wakhungu, wosawuka, watsoka, ndipo sudziwa konse zimenezo.”

²²⁹ Tsopano, ngati munthu anali wamaliseche, kunja uko pa msewu, ndipo akanadziwa icho, bwanji, iye akanayesa kudzithandiza yekha. Koma pamene iye—pamene iye sakudziwa izo, ndipo iwe sungakhoze kumuwuza iye kusiyana kulikonse, ndiye iye ali mu chikhalidwe choyipa. Mulungu achitire chifundo pa iye. Kulondola. Zindikirani. O, mai!

²³⁰ Tsopano, kumbukirani, wotsutsakhristu uyu, mwiniwake, pokhala mwamuna; mkwatibwi wake, amene ali mpingo wake, “anapatsidwa danga kuti alape, ndipo iye sanachite zimenezo,” mu m'badwo wa mpingo umenewo, Tiyatira. Inu mukukumbukira izo? Mungakhoze inu. . .

²³¹ Chabwino, tiyeni tibwerere mmbuyo miniti chabe. Sizitipweteka ife kubwerera mmbuyo miniti chabe. Tiyeni tibwerere mmbuyo, kwa mutu wa 2, miniti chabe. Ife tingowerenga icho, mutu wa 2 wa. . . tsopano, Tiyatira. Tsopano yang'anani ichi, basi mwamsanga kumene tsopano. Mai, ife tiri pafupi nthawi yotsekera, ndipo sitinafike poyamba. Koma, zindikirani, Tiyatira. Tsopano, izo zikuyambira pa ndime ya 18 ya m—mutu wa 2.

. . . kwa mngelo (ndiye mtumiki) wa mpingo mu Tiyatira lemba; Zinthu izi anena Mwana wa Mulungu,

amene ali nawo maso ake monga malawi . . . ndi mapazi ake monga mkuwa wonyezimira;

Ine ndidziwa ntchito zako, ndi chikondi chako, ndi utumiki wako, ndi chikhulupiro chako, . . . chipiriro chako, ndi ntchito; ndipo iwe uyenera kukhala mochuluka kuposa . . . ndipo zotsiriza kukhala zochuluka zuposa zoyamba.

Komabe ine ndiri nazo zinthu pang'ono zotsutsa iwe, chifukwa iwe ukulola mkazi uja Yezebeli, . . .

232 Ndi zimenezotu. Inu mukumudziwa iye, mu Baibulo. Iye anali mkazi wa Ahabu. Ndipo apa pali mkazi, mpingo, Yezebeli, mkazi wa mneneri wabodza, amene akuyenera kukhala mneneri weniweni wa Mulungu, papa; kulondola, mneneri weniweni ndi mkazi wake, Yezebeli. Tsopano, Ahabu ankayenera kukhala Myuda weniweni, koma iye anali mthakati, inu mukudziwa zimenezo, chifukwa mkazi wake ankangomutsogolera iye njira iliyonse imene iye ankafuna kutero. Ife tikupeza kuti, Yezebeli akutenga ndalama zake ndi kuwatsogolera awa njira yomwe iwo akufuna kutero, nayenso.

. . . yemwe adzitcha yekha mneneri wamkazi, (mwamva izo?), kuti aphunzitse ndi . . . kufooketsa antchito anga (mukuwona, kuphunzitsa uko kwa Yezebeli kunangosesa dziko) kuti achite ziwerewere ndi . . . kudya zinthu zoperekedwa nsembe kwa mafano.

. . . ine ndinampatsa iye danga kuti alape (mukuwona?) za ziwerewere zake; ndipo iye sanalape ayi.

233 Yang'anani ndime yotsatira iyi.

. . . ine ndidzamuponya iye pa kama (ndiyo gehena), ndi iwo amene achita chigololo naye iye kuwalowetsa ku zisawutso zazikulu, . . . (Ndiko kukalowa mu Chisawutso chachikulu. Osati Mpingo, tsopano.) . . . pokha iwo atalapa za machitidwe awo.

234 Tsopano yang'anitsitsani, apa.

. . . ine ndidzapha ana ake (timahule take) ndi imfa (imfa yauzimu); . . .

235 Inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ndiwo Mawu. "Ine ndidzawapha iwo ndi imfa." Ndipo ngati iwo apedwa, iwo alekanitsidwa Mwamuyaya. Chabwino. Kumbukirani, Iye anamupatsa iye danga kuti alape.

236 M'badwo wa Tiyatira unali m'badwo wa mdima. Wokwera pakavalo wakuda ankakwera mu nthawi imeneyo, pamene misa zonse ndi chirichonse zinkayenera kulipiridwa, ndi mapemphero, ndi—ndi manovena, ndi zina zotero. Tsopano onani kavalo wakuda wake, ndiye, atatha iye kukana kulapa

mu Tiyatira, (chiyani?) akusintha kukwera kwake kuchoka ku kavalo wakuda kupita kwa mmodzi wotumbululuka, imfa, kwa utumiki wake wotsiriza.

²³⁷ Tsopano, ine ndikhoza kungomupatsa aliyense kugwedeza pang'ono apa. Kukana Mulungu, kukana kuyitana kwa Mulungu, inu mudzachita izo kwa nthawi yotsiriza nthawiyina. Ndipo, monga momwe mpingo uja unachitira, iwo unatha. Mulungu, chipiriro, nthawizonse sadzalimbana naye munthu. Mukuwona?

²³⁸ Ndipo pamene iye anawakana Iwo, ndipo atakana kuwalandira Iwo, ndiye iye anasintha ndipo anapita . . . Tsopano iye ali nalo dzina lotchedwa “Imfa,” kulekanitsidwa. Mulungu anati, “Ine ndidzatenga ngakhale ana ake, Aprotostanti, ndi mmodzi aliyense wa iwo ine ndidzamupha ndi kulekanitsidwa Mwamuyaya.” Ndi zimenezotu, M'badwo wa Tiyatira, m'badwo wa mdima. Kavalo wakuda wake tsopano akutembenukira ku imfa, ku utumiki wake wotsiriza.

²³⁹ Onani momwe mibadwo ya mpingo ikulumikizirana nazo Zisindikizo? Mwangwiro basi. Ndipo ife tikudziwa kuti Izo nzolondola. Mzimu Woyera sumalakwitsa. Iye anatipatsa ife chitsimikiziro chachikulu, nthawi yathayo, pamene ife tinatsiriza mibadwo ya mpingo mmbuyo umo, inu mukudziwa.

²⁴⁰ Mukuwona kukonda, kopirira-motalika kwa Mulungu! Iye asanapereke chiweruzo pa iye, Iye anamupatsa iye malo kuti alape. Ndipo ziri mu Dzina la Ambuye ine ndikunena izi: Iye wawupatsa mpingo wa Chiprotostanti chinthu chomwecho, ndipo iye sachita izo. Uthenga wagwedeza paliponse, ndipo iye sachita izo. Iye akhala nayo miyambi yake ndi zikhulupiriro, ine sindikusamala kaya inu mulongosola chotani Izo.

²⁴¹ Monga ine ndinanena uko mu Chicago, tsiku lina, kwa atumiki ambiri kuposa anthu amene akhala pano! Ndipo kumeneko iwo anandipanikiza ine, pa Chiphunzitsa, cha mbewu ya serpenti ndi chinthu china chonse ichi. Ine ndinati, “Wina atenge Baibulo lako, ndipo bwera apa ndi kudzayima pambali pa ine ndiye.” Ndipo palibe aliyense ananena kanthu.

²⁴² Tommy Hicks anati, “Ine—ine sindinamvepo Izo monga choncho nkale, M'bale Branham. Ine ndikufuna mazana atatu a matepi amenewo. Ine ndikawatumiza iwo kwa azitumiki anga onse.”

²⁴³ Apo panali pafupi makumi asanu, kapena makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu, anati, “Ine ndikubwera kumeneko kudzabatizidwanso.” Kodi iwo anabwera? Osati mmodzi wa iwo. Chifukwa? Iye anawapatsa iwo danga kuti alape! Ndipo Iye adzaponyera ana anu ku imfa, imfa yauzimu.

²⁴⁴ Ife tidzatenga izo mawa usiku, Ambuye akalola, kapena Loweruka usiku, pa Miliri imeneyo imene ikudutsa pamenepo. Inu muwone zimene zikuchitika pamenepo.

245 Monga Iye anapatsa Igupto, Iye anapatsa Igupto malo kuti alape. Ndipo mliri wotsiriza uwo unali chiyani? Unali imfa.

246 Ndiwo mliri wotsiriza umene wagunda mpingo wa Chipentekoste, ndiwo imfa yauzimu. Iye ali wakufa. Ndizo mu Dzina la Ambuye. Iye ali wakufa mwauzimu. Iye anamupatsa iye malo kuti alape, ndipo iye anawakana Iwo. Tsopano iye ali wakufa. Iye sadzawuka konse kachiwiri.

247 Ndipo anthu awo kunja uko, kuyesera kulowetsamo ma Episcopalia ndi ansembe, ndi ena otero, ndi kumawatcha iwo “Bambo Woyera *Wakuti-ndi-wakuti*.” Bwanji, iwo ayenera kudzichitira manyazi okha. Munthu angakhale bwanji wakhungu? Kodi Yesu sakutero? Pamene namwali wogonayo abwera kuti agule Mafuta, iye sanawapeze Iwo!

248 Aliyense, inu mumamva anthu akuti, “Ine ndiri nawo Mzimu Woyera. Ine ndinalankhula mu malirime.” Koma iwo sakufuna kubwera ku mpingo monga uwu. “O, inu mukudziwa, ine sindikukhulupirira ine ndikufuna kumapita pafupi ndi malo ngati amenewo.” Ndiyeno kumati inu muli nawo Mzimu Woyera?

249 Koma inu mukufuna njira zanu zolemekezeka. Inu mukufuna kukhala mu Babeloni ndi kumasangalalabe nawo madalitso a Kumwamba. Inu muyenera kupanga kusankha kwanu. Inu simungakhale kunja uko mu dziko ndi kumamutumikira Mulungu pa nthawi yomweyo. Yesu anati inu simungakhoze kutumikira Mulungu ndi mamoni. Kotero ngati inu simungayembekeze . . .

250 Ngati iwe wapulumutsidwa kwenikweni, iwe uzisangalala nayo misonkhano pamene Mzimu Woyera ukudzitsimikizira Wokha ndi kuwonetsa kuti Mawu a Mulungu ali choncho.

251 Winawake anati, “Anthu amasokosera kwambiri. Izo zimandipangitsa ine manjenje.” Inu mudzakhala amanjenje ngati inu muti mudzakafike Kumwamba. Ndipo iwe ingoganiza, pamene iwo onse adzakhale kumeneko, ndiye nanga bwanji zimenezo? O, mai! Momwe Ambuye akufunira kutenga . . .

252 Iye ali wopirira-motalika, monga Iye analiri mu masiku a Nowa. Iye anayetsa molimba. Iye anapirira motalika, kwa zaka zana ndi makumi awiri, kuti awafikitse iwo ku kulapa. Iwo sakanachita izo.

253 Mu masiku a Igupto, Iye anatumiza mliri ndi china chirichonse. Iwo sakanachita izo.

Iye anatumiza Yohane. Iwo sakanabwerera.

254 Iye anatumiza Yesu, kudzafa, kudzapulumutsa gulu lonse limene likanadzamva Mawu.

255 Ndipo tsopano, mu masiku otsiriza, Iye analonjeza kachiwiri kuti Iye adzatumiza Uthenga kuti umuyitanire Iye kunja, ndi kubwezeretsa Chikhulupiriro chapachiyambi kubwerera kwa Iwo, kubwerera ku Mawu. Ndipo iwo sawalandira Iwo. Iwo ali

a mu miyambi kwambiri, mu miyambi yawo ndi zikhulupiro, mpaka iwo sakuwafuna Iwo. O, iwo amaganiza ngati iwo akanakhala. . . ngati Mngelo akanayenda pansu; koma Mulungu samachita zimenezo.

²⁵⁶ Iye amatenga chinachake chopulikira ndi chopusa, chinachake chimene sichidziwa nkomwe ABC wanu kapena—kapena chirichonse. Ndiyeno Iye amatenga munthu wa mtundu umenewo, chifukwa Iye akhoza kutenga chinachake chimene chisali kanthu ndiyeno nkugwira ntchito kupyolera mu chimenecho. Malingana ngati chinachake chikuganiza kuti iwo ali chinachake, ndiye iwo sangachite kanthu nacho icho. Iye nthawizonse amachita zimenezo. Inu muyenera kusakhala kanthu, kuti mukakhale winawake ndi Mulungu. O, mai!

²⁵⁷ Zindikirani, komabe, “Iye anamupatsa iye danga kuti alape, koma iye sanachite izo.”

²⁵⁸ Iye wachita icho kachiwiri; iye sachita izo. Kukana kwake, kutali, kukumupanga iye. . . Kapena, kukana kwake kukupanga njira yangwiro kwa Satana kuti alowe mwa iye ndi kukhala mu thupi. Uko nkulondola. Kudzikhazika mu thupi yekha mwa iye, chifukwa iye anawakana Mawu. Ndipo ndicho chimodzimodzi chinthu chomwecho chimene mpingo wa Aprotostanti ukukhala, kahule, ndi chifukwa chakuti iwo ukukana Chwonadi chotsimikiziridwa cha Mawu a Mulungu, ndipo icho chikumupatsa Mdierekezi malo akuti alowere mkati momwe ndi kudzadzikhazika mu thupi yekha. Ndipo iye apanga fano kwa chirombo pamene iwo anagwirizana pamodzi, kutsidya uko tsopano, ndipo kumangopita momwemo zomwe Iye ananena. Uko nkulondola. Amen.

²⁵⁹ Ngati ine ndikanakhala nawo maphunziro, ine ndikanakhoza kuzitulutsa Izo panja. Ine ndiribe maphunziro. Ine ndikungoyembekezera Mzimu Woyera kuti uziwululire Izo kwa inu. Ndipo Iye adzatero, kwa iwo amene. . . Uko nkulondola. Iye adzachita izo. Inde. Zindikirani.

²⁶⁰ Yang’anani momwe, chimene iye anachita apa. Iye anakana Uthenga wa Mulungu kuti iye alape. Iye anayambapo, wotsutsakhristu, ndipo ndicho chimene iye anali. Iye anabwera, mneneri wabodza, Mdierekezi mu thupi, ndipo, pamene iye anatero, ndi kuphunzitsa kwabodza kwake. Ndiye, mu zonse za izo, Mulungu anamupatsa iye danga kuti alape, kuyesera kumutenga iye.

²⁶¹ Mukuwona kupirira-motalika kwake? Chikondi chodabwitsa chotani! Palibe chikondi monga chimenecho! Yang’anani pa iwo, ngakhale amene analavulira mu nkhope Yake ndi zinthu, Iye anawakhululukira iwo. Ndiye Mulungu, mukuwona. Musati. . .

²⁶² Kukana Uthenga wa Mulungu! Yang’anani, iye anafunsidwa kuti alape, kubwerera kumene iye anagwa kuchokera.

263 Ndipo iye anagwa kuchokera ku chiyani? Mawu. Kulondola. Eva anagwa kuchokera ku chiyani? [Osonkhana ati, “Mawu.”—Mkonzi.] Mawu! Chipembedzo chinagwa kuchokera ku chiyani? [“Mawu.”] Ndi zimenezotu. Mukuwona? Palibe njira yina. Basi, nthawi iliyonse, kubwerera kumene ku Mawu, kubwerera kumene ku Mawu. Mukuwona? Ndipo iwo akulowa mu kachitidwe kamene kakuwachotsa iwo ku Mawu, kuwachotsa iwo kuchokera ku Mawu mmalo mopita ku Mawu. Zindikirani.

264 Onani, iye anapatsidwa danga kuti alape, kupita mmbuyo. *Lapani* kumatanthawuza “kupita mmbuyo, kutembenukira mmbuyo, kutembenuza-nkhope.” *Lapani*, “kupita mmbuyo.” Ndipo iye anapatsidwa danga kuti abwerere kumene icho. . .

265 Tsopano kumbukirani, iye anali wapachiyambi, Mpingo wa Chipentekoste umene Mzimu Woyera unatsanuliridwapo, pa Tsiku la Pentekoste. Ndi angati ophunzira Baibulo amadziwa zimenezo? Ndithudi, iye anali. Penyani pamene iye anachokera? Iye anagwa kuchokera ku Mawu, ndipo analandira miyambi. Iye ankayembekezera. . .Mmalo mwa Mzimu Woyera, iye ankafuna munthu woyera, “Dokotala L L., Ph., Q. U.” ndiyeno anamupanga iye papa. Mukuwona? Ndithudi. Koma, iye, ndicho chimene iye ankafuna, winawake woti azimupempherera iye. Winawake. . .Iye amangolipira ndalama zake, ndipo ndicho chonse iye ankayenera kuchita. Mukuwona?

266 Tsopano, ndicho chinthu chomwecho lero. Basi malingana ngati iwo ali nawo mpando woti akhalepo, kupereka molemerera pa mbale yosonkhetsa, ndicho chabwino mokwanira. Iwo ali chiwalo cha mpingo umenewo. Musati muwawuze iwo kanthu kalikonse za Iwo; iwo sakufuna kuti adziwe. Ndiwo ana aakazi ake.

267 Tsopano, iye anagwa kuchokera ku chiyani? Kuchokera ku Mawu apachiyambi autumwi a atumwi ndi aneneri. Ndiko kumene iye anagwa kuchokera. Ndiko kumene Aprotetanti anagwa kuchokera.

268 *Lapani!* Pitani mmbuyo! Tembenukirani mmbuyo nthawi isanathe. Sikunakhale mochedwa kale. Limodzi la masiku awa Mwanawankhosa uyo adzasiya malo Ake, ndiyeno zonse zathera pamenepo. Kotero ali ana aakazi ake kufunsidwa tsopano, asanati aweruzidwe ndi iye, kuti “atembenukire mmbuyo.”

269 Tsopano, Uthenga wotsiriza umene iwo ali nawo, uli pamene mneneri uyu amene ine ndakhala ndikumunena. Yemwe, ine ndakhala ndikuwerenga mabuku ambiri za izo. Ndipo ine ndikudziwa kuti anthu enieni, abwino, oganiza, oganiza-mwauzimu amadziwa kuti izo zikubwera. Iwo amadziwa izo. Iwo amadziwa kuti izo zikubwera, mwawona. Iwo. . . Koma vuto lake, liri, iwo amakhala akunena, “Ife tikuzifuna izo. Izo zidzakhhalapo.” Ndipo pamene Icho chibwera, kuti

iwo adzakhale odzichepetsa kwambiri; iwo mwinamwake adzachiphonya Icho monga momwe iwo anachitira nthawi yina. Uko nkulondola. Anthu adzalemba za Icho, ndi chirichonse, kunena, “O, inde, izo ziyenera kukhala.” Ndiyeno mulole Icho chiwonetsedwe pamaso pawo pomwe, ndipo iwo amangopitirira chonchobe, mwawona. Kotero, iwo nthawizonse achita izo.

²⁷⁰ Yang’anani tsopano, Mawu apachiyambi. Iwo ku... iwo... Iye ayenera kulapa, kuti apite mmbuyo, komabe, kotero ana aakazi ake afunsidwa. Kuti akakamidzidwe... iwo adzaweruzidwa, ndi kuponyedwa mu kama yemweyo ndi kuphedwa limodzi naye iye. Iwo afunsidwa kuti abwerere mmbuyo ku Mawu apachiyambi, kubwerera ku Chiphuzitso cha utumwi. Koma, iwo ali omangidwa kwambiri pansu ndi zikhulupiriro zawo ndi zinthu, iwo sachita izo. Iwo angochitonza Icho.

²⁷¹ Ndiye iwo akuchita chiyani? Iwo potsiriza akugwirizana mu fano kwa chirombo, mphamvu yina; zindikirani, ndi kuchita, kwa Mkwatibwi wa Mwanawankhosa, monga iye anachitira mu Chivumbulutso 13:14. Ndicho chimene iwo akuchita, kumangozunza, basi chinthu chomwecho. Mipingo imangotonza basi Mkwatibwi woona wa Khristu, monga Roma wakhala akuchitira. Chimodzimodzi basi. Inde, bwana. Machitidwe kwa—Mkwatibwi weniweni wa Mwanawankhosa chimodzimodzi basi monga iye anachitira mu Chivumbulutso 13:14.

²⁷² Tsopano zindikirani. Ife tikuwona, mwa Mawu a Mulungu a lonjezo, Iye adza—Iye adzapha ana ake, zipembedzo, ana ake aakazi, ndi imfa yauzimu. Tsopano, ndicho Chivumbulutso 2:22. Musati muyiwale izo. Kupha, ndiko kuyika ku imfa. Ndipo *imfa* ili “Kulekanitsidwa Mwamuyaya ndi Kukhalapo kwa Mulungu.” Ganizani za icho, amzanga. Ganizani za icho. Musati inu mudalire mu zikhulupiriro zirizonse zopangidwa ndi munthu. Chirichonse chimene chiri chosiyana ndi Mawu, inu mukhale kutali kwa icho.

²⁷³ Tsopano yang’anani, yang’anani mu Baibulo apa. Ilo linati dzina lake linali Gehena, ndipo... Ine ndikutanthawuza:

... dzina lake *linali Imfa, ndipo gehena inamutsatira iye.*

²⁷⁴ Tsopano, gehena nthawizonse imatsatira imfa, mwachibadwa. Pamene munthu wachibadwa amwalira, gehena imamutsata iye; ndiwo manda, hade, mwawona, ndizo mwa chibadwa. Koma mwauzimu, ndiyo Nyanja ya Moto, mwawona, chabwino, kulowa mu kulekanitsidwa Mwamuyaya, kumene iwo akuwotchedwa.

²⁷⁵ Ndipo—ndipo Malaki 4 anati, “Osawasiyira iwo ngakhale chiputu kapena nthambi, kapena kanthu kalikonse.” Ndiyo njira

yomwe dziko liri nako kudziyeretsera ilo lokha apanso, kuti kukhale Zakachikwi. Mukuwona?

²⁷⁶ Kodi inu mwazindikira, wokwera ali “iye”? Ndipo “iye” anali nalo mu mdzanja “lake”; “mwamuna,” mneneri wabodza. Koma mkwatibwi wake akutchedwa mpingo, “mkazi,” Yezebeli. Ahabu; Yezebeli. Bwanji, chiri chabe mwangwiro monga chirichonse. Mukuwona? Mukuwona?

²⁷⁷ *Ana aakazi* ali “akazi,” nawonso, koma sanalandire konse ulamuliro wa mwamuna mmodzi; Aprotestanti, kwa uyo, komabe kahule mu kachitidwe, ka chiphunzitso chawo, chipembedzo, machitidwe. Ndizo chabe. . . Ndizo zimene ilo limanena.

²⁷⁸ Zindikirani. Zonse izi zikubwera pati? Tsopano, ife tiri nawo chabe pafupi khumi ndi awiri, maminiti khumi ndi anai apa, ine ndikuganiza. Onani kumene zonse izi zikubwera. Nchiyani icho? Izo zikubwerera mmbuyo kumene momwe izo zinachitira, ndipo zinayambira Kumwamba. Izo zikufika ku nkhondo ya nthawi yotsiriza.

²⁷⁹ Chinthu choyamba, Kumwamba, chinali nkhondo. Lusifala anakankhidwa kunjja, ndi kubwera ku dziko lapansi. Ndiye iye anawononga Edeni; ndiye iye wakhala akuwononga kuyambira pamenepo. Ndipo tsopano, kuchokera ku nkhondo ya Kumwamba, zikubwera ku nkhondo pa dziko lapansi; ndipo iyo ili yoti itsirizikire ku, pa dziko lapansi, pa nthawi yotsiriza, mu nkhondo yotchedwa Armagedoni. Tsopano, aliyense amadziwa zimenezo. Nkhondo inayambira Kumwamba, woyera, ndipo kotero iwo anamukankhira iye panja. Mikaeli ndi Angelo Ake anamugonjetsa iye, anathamangitsidwa. Ndipo pamene iwo anatero, anatsikira komwe ku Edeni, ndipo apa anayamba nkhondo pansa apa. Kum. . .

²⁸⁰ Mulungu anali nawo ana Ake otetezedwa ndi Mawu Ake. Ndipo Eva anatulutsa khosi lake kunjja, anati, “Ine ndikukhulupirira iwe ukulondola, mwinamwake.” Ndipo pamenepo iyo inayamba. Ndipo iyo yakhalapo, kuyambira pamenepo. Ndiye Mulungu anabwera pansa, ndipo tsopano Iye ayenera kuti. . . Iye anabwera pansa kudzawombola iwo amene akanadzabwera pansa.

²⁸¹ Monga ine ndinanenera, Mulungu ali ngati womanga wamkulu. Iye amayika zida Zake zonse pa dziko lapansi, ndiyeno Iye amamanga nyumba Zake. Tsopano kumbukirani, apo pasanakhale njere ya—ya mbewu pa dziko lapansi, pasanakhale dzuwa lomwe linakanthapo dziko lapansi, thupi lanu linali kugona pa dziko lapansi, chifukwa inu muli fumbi la dziko lapansi. Mukuwona? Inu muli. Mulungu ali womanga.

²⁸² Tsopano, njira yomwe Iye amakachitira izo, inali kufika pansa ndi kutenga (monga Iye anachitira Adamu) gulu laling’ono la kashiyamu, potashi, ndi kuwala kwa dziko, ndi, “Psyiii!”

Kunena, “Apo pali mwana Wanga wina.” Mukuwona? Ndiye nkubweretsa zina zochulukira, ndi, “Psyii!” “Apo pali mmodzi wina.”

²⁸³ Koma Eva anachita chiyani? Iye anawononga njira imeneyo. Ndipo iye anayibweretsa iyo kupyolera mu mchitidwe wa kugonana, ndiye imfa inakantha izo.

²⁸⁴ Tsopano Mulungu akuchita chiyani? Iye ali nazo zochulukira za mbewu zimenezo pansi kupyola kumeneko, ndiyo yokonzedweratu; yochulukira chonchi, yokonzedweratu. Ndiyeno, pa nthawi yotsiriza, Iye sadzanena kuti, “Eva, bwera udzabale mwana wina.” Iye (“Psyii!”) adzayitana, ndipo ine ndidzayankha. Ndizo zonse. Ndi zimenezotu. Ndilo lingaliro. Pamene mmodzi wotsirizayo walowetsedwa mkati, icho chikhazikitsa izo.

²⁸⁵ Tsopano, nkondo inayambira Kumwamba. Iyo idzatsirizikira pa dziko lapansi, mwa mawonekedwe a Armagedoni.

²⁸⁶ Tsopano tiyeni tiyang’ane ndipo tichiwone icho chikufutukuka. Ndipo mwinamwake ife tikhoza kuchifutukula icho. Ambuye atithandize ife pakali pano kuti tichite ichi tsopano. Penyani icho chikufutukuka.

²⁸⁷ Wokwera wachinsinsi, yang’anani chimene iye akuchita tsopano; “anatsutsa,” anakana kulapa ndi kuti abwererenso ku Mawu Amagazi apachiyambi. Mawu anakhala Magazi ndi thupi. Mukuwona? Iye anakana kubwerera kwa Iwo. Ali wotsutsakhristu! Mkwatibwi wa Mawu owona, ali wotsu-... iye ali wotsutsa kwa Mkwatibwi wa Mawu owona. Akutenga mkwatibwi wakewake! Iye akutsutsana naye Mkwatibwi woona uyu, nayanenso. Ndipo iye akutenga mkwatibwi wakewake, ndi kumubweretsa iye kwa iye, mwa mawonekedwe a chipembedzo chotchedwa zikhulupiriro ndi miyambi. Mukuwona? Ndipo tsopano, powona Mkwatibwi woyera, iye ali kutsutsana naye Iye. Koma iye akupanga mkwatibwi wakewake, wotchedwa wotsutsakhristu, mwa kuphunzitsa kotsutsakhristu, kumene kuli kosagwirizana ndi Khristu. Mukuwona momwe iye aliri wothe yathyalika? Ndipo tsopano, mmalo mokhala nawo umodzi wa chikondi, kulamulira, kupembedza pansi pa Magazi, iye ali nacho chipembedzo. Mmalo mokhala nawo Mawu, iye anatenga zikhulupiriro, miyambi, ndi zina zotero.

²⁸⁸ Monga, ndipo Achiprotestanti amati, “Chikhulupiriro cha Atumwi.” Ine ndikufuna inu mupeze mawu a icho mu Baibulo. Atumwi, mulibe Chikhulupiriro cha Atumwi mu Baibulo.

²⁸⁹ Monga ine ndinanena apa, tsopano, osati kale litali, kapena kwinakwake. Ngati atumwi anali nacho chikhulupiriro, chiri Machitidwe 2:38. Chimodzimidzi basi chonse chomwe ine ndikudziwa iye anali nacho konse. Ndicho chimene iwo ankayitanira aliyense kuti achite. Pamene iye anapeza mmodzi

wa iwo amene ankawoneka ngati iwo anali Akhristu, iye anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene munakhulupirira?”

Anati, “Ife sitikudziwa kaya kuti kuli . . .”

Anati, “Ndiye inu munabatizidwa chotani?”

²⁹⁰ Tsopano, kukhala obatzidwa mu Dzina la Yesu, kapena mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, kani, izo, izo nzabwino, koma sindizo zonse za izo apobe. Ayi, bwana. Inu mukhoza kubatizidwa nthawi makumi asanu, monga choncho, ndipo nkusachita pang’ono ubwino mpaka mtima umenewo utasinthidwa ndi Mzimu Woyera. Izo zonse ziyenera kupita limodzi. Zindikirani, ndi—ndi Khristu!

²⁹¹ Wotsutsakhristu akukana Chiphunzitso cha Mkwatibwi woota, ndipo chotero iye akutenga mkwatibwi wakewake tsopano ndi kumumangira iye, pansi pa chikhulupiriro chakechake. Kutenga mkwatibwi wakewake ndi kumupanga iye chipembedzo! Iye akubala zipembedzo zina, monga zalembedwa mu Malemba awa Oyera; akubala ana aakazi. Ndipo iye sati . . . Iye akukhala monga ngati mayi wake, wachibadwa, wachidziko, wachipembedzo; kutsutsa Mkwatibwi wauzimu, Mawu.

²⁹² Iwo samati iwo sali a mu mpingo. Inu mukalankhula kwa munthu wachipembedzo. “Ndithudi, ine ndiri wa mu mpingo.” Kodi ndinu Mkhristu? “Ine ndiri wa nu mpingo!” Icho chiribe chinthu chimodzi chochita nawo Iwo! Iwo amati . . . Inu simuli a Mpi- . . . Inu, inu mukhoza kukhala wa mu chimene chimatchedwa mpingo, mwawona, kukhala wa mu mpingo. Umenewo si Mpingo. Iyo si ili Mipingo. Izo ndi mphanga kumene anthu amasonkhana pamodzi, ndipo anthu monga, “mbalame za nthenga zofanana.”

²⁹³ Koma inu muli Mpingo umodzi wokha, ndipo ndiwo Thupi lachinsinsi la Khristu. Ndipo inu simumawujowina Iwo. Inu mumabadwira mwa Iwo.

²⁹⁴ Monga ine ndakhala ndikunena nthawizonse, ine ndakhala mu banja la Branham zaka makumi asanu ndi zitatu, ndipo sindinajowine konse ilo. Ine ndinabadwira mmenemo. Mukuwona?

²⁹⁵ Tsopano zindikirani. Izo zikungofanizidwa mokongola. Ine—ine ndiri nalo . . . Lemba lolembedwa pansi apa, koma ine . . . ife tiribe nthawi kuti tifike kwa ilo; monga Esau ndi Yakobo.

²⁹⁶ Tsopano, Esau anali munthu wachipembedzo. Iye sankadzitcha kuti ali wosakhulupirira. Iye ankakhulupirira mwa Mulungu yemweyo Yakobo ankakhulupirira, Mulungu yemweyo abambo ake ankakhulupirira. Koma iye anali chabe shyashya, kapena pepani katchulidweko, chabe . . . Iye anali chabe wopanda pabwino. Iye—Iye anali, tsopano, polankhula za kukhala wamakhalidwe, iye anali kwenikweni—munthu

wakuchita-mwamakhalidwe abwino kuposa Yakobo analiri. Koma, inu mukuwona, iye sanaganize. . . “O, ufulu wobadwa nawo uli nacho chochita chanji ndi Ichu?” Ndipo iye anagulitsa ufulu wake wobadwa nawo kwa Yakobo. Mukuwona?

²⁹⁷ Koma, Yakobo, iye analibe zinthu zazikulu, ndipo monga Esau analiri. Iye analibe cholowa chomwe iye anali nacho. Koma apo panali chinthu chimodzi chimene Yakobo ankachifuna, chinali ufulu wobadwa nawo uja. Iye sankasamala momwe iye angadzapezere iwo; iye akanadzawupeza iwo. Ndipo Mulungu anali nako kulemekeza kwa iye.

²⁹⁸ Ndipo, ndiye, ndicho chinthu chomwecho lero, ndi munthu wachibadwa, malingaliro amwathupi, wolingalira-mwadziko. “Chabwino, ine ndine wa mu mpingo wa boma. Ine ndine wa mu mpingo *uwu*. Ine ndine wa *uwu*.” Izo ziribe chinthu chimodzi chochita nawo Iwo, palibe chinthu.

²⁹⁹ Yang’anani, akuwasonkhanitsa iwo tsopano pa kavalo wake wa mitundu-yosanganikirana. Iye akuwasonkhanitsa iwo pamodzi, pa kavalo wake wa mitundu-yosanganikirana, chifukwa iye ali nayo mphamvu ya ndale.

³⁰⁰ Inu simukukhulupirira kuti iye ali nayo? Purezidenti uyu walowamo bwanji tsopano pompa? Zimenezo zinapulumuka motani? A-nha! Kubwera kuno chifukwa cha ufulu wa chipembedzo; ndipo inu gulu la ademokirati limene likanagulitsa maufulu obadwa nawo anu ku ndale! Ine ndiribe. . . Chipani cha Demokirati ndi chabwino; izo zonse ndi zovunda. Ine ndikulankhula za Chikhristu. Koma inu mukugulitsa maufulu obadwa nawo anu, pa tiketi ya Demokirati, kuti muyike chinachake monga chimenecho mkati. Manyazi pa inu!

³⁰¹ Kodi inu simukuzindikira kuti fuko lino, chimodzimodzi, liri mu dongosolo la Israeli? Israeli anachita chiyani? Iye anabwera ku dziko lachirendo uko, ndipo anawatengera okhalamo kunja ndipo anawapha iwo, ndipo analowamo ndi kutenga dzikolo. Ndicho chimene ife tinawachita; Amwenye. Ndi okhawo Amerika owona amene alipo, ali amzathu a Chimwenye.

³⁰² Ndiyeno iwo anachita chiyani? Israeli anali nawo amuna pang’ono opambana. Chinthu choyamba inu mukudziwa. . . Iwo anali naye Davide, ndipo iwo anali naye Solomoni. Iwo anali nawo amuna opambana. Ndipo potsiriza iwo anatenga chigawenga kuntunda uko, Ahabu, amene anakwatira Yezebeli, wosakhulupirira.

³⁰³ Chabwino, ndicho chinthu chomwecho chimene ife tinachita. Ife tinali naye Washington ndi Lincoln, koma yang’anani chimene ife tiri nacho tsopano. Ndipo chinthu chomwecho cha ichu, chiri, iye wakwatira, ndi kugwera pansu ndi kulochedwa-mu-ubweya kwa Yezebeli. Iye akhoza kukhala mnyamata wa mtundu wokongola bwino, koma mkaziyo ndiye

ati ayendetse malonda. Ndipo inu mukuziwona izo pakali pano, banja lonse likubwera mkati.

³⁰⁴ Mzimu Woyera unandiwuza chiyani ine, pafupi zaka makumi atatu ndi zisanu zapitazo? Ndipo inu nonse a masiku akale mukudziwa zimenezo, za zinthu zisanu ndi ziwiri zimene zikanadzachitika asanafike matsiriziro. Ndipo ichi chiri chotsiriza, chotsatira kwa chinthu chotsiriza, chimene chikubwera. China chirichonse chinangogunda chimodzimodzi pa dontho, ku nkondo ndi china chirichonse. Mukuwona? Ndipo tsopano iye ali mmanja kumene, mkazi, kuti alamulire fukoli. Yezebeli! Mukuwona?

³⁰⁵ Koma, kumbukirani, mu masiku a Yezebeli, winawake kwenikweni anawawuza iwo mitundu yawo. Mukuwona?

³⁰⁶ Kusonkhana, pa kavalo wawo wamitundu-yosanganikirana. Ndipo, onani, iye ali kusonkhanitsa chinthu ichi pamodzi, chosanganikirana ndi zikhulupiriro, chipembedzo, ziphunzitsi zopangidwa ndi anthu. Nkulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndithudi, mtundu wosanganikirana, mtundu wosanganikirana wa kavalo wotumbululuka, wakufa wa mdziko! Tsopano, uko nkulondola. Mitundu yosanganikirana ya kavalo wakufa, mawonekedwe a chidziko a kavalo wotumbululuka, o, mai, wopanda Magazi oyera a Mawu, konse!

³⁰⁷ Ndipo yang’anani. Kuchokera ngodya... “Kuchokera ku ngodya zinai za dziko lapansi, iwo akuwasonkhanitsa iwo; kuwasonkhanitsira iwo ku Armagedoni,” Baibulo linatero. Ine ndikuyesa kuganiza za Malemba, monga ine ndawalemba iwo pansu apa. Ine sindikuwatchula iwo; koma chabe pamene iwo alembedwapo, kuwona chimene iwo ali. “Kuwasonkhanitsa iwo pamodzi, ku tsiku lalikulu la nkondo ya Ambuye Mulungu.” Yang’anani. Tsopano, pa kavalo uyu wamitundu-yosanganikirana, wachidziko, wotumbululuka, kavalo wodwala, tangoganizani za izo; inu mukudziwa, ndicho chinthu choyipa. Tsopano yang’anani kumene iye akuwasonkhanitsira iwo, “Kuchokera ku ngodya zinai za dziko lapansi.” Iwo akusonkhanitra tsopano ku chiwonetsero. Chiwonetsero chidzakhala pa “Armagedoni,” malingana ndi Mawu. Mukuwona?

³⁰⁸ Pa kavalo wotumbululuka, atakwera pa iye, ndi “Imfa” itayikidwa... ndi dzina litayikidwa pa iye, “Imfa,” wotsutsakhristu! Tamverani. Wotsutsakhristu, chipembedzo choyamba (icho sichingakanidwe); ndi Yezebeli wake, wadama kwa Mawu; ndi ana ake aakazi, ndi iye, Aprotostanti; kudzisonkhanitsa okha pamodzi tsopano mu umodzi!

³⁰⁹ Kodi inu munawamva anthu Achibapatisti akulankhula tsiku lina cha kuno, inu mukudziwa? Ha? “O, ife sitijowinana nawo iwo, koma ife tidza—ife tidzakhala pachibwenzi ndi kukhala ngati kuvomerezana nawo iwo. Ife sitikusowa kujowina

mpingo wawo, koma . . .” Ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu, chimodzimodzi basi chimene Mawu ananena. Mukuwona? Mukuwona? Hule lakale, mu malo oyamba, mwawona.

³¹⁰ Tsopano apa iwo ali, kudzilumikiza okha pamodzi, kubwera ku chiwonetsero icho, ku Armagedoni, ndi kukwera pa kavalo wamitundu-yosanganikirana; ndi kavalo mmodzi woyera, kavalo mmodzi wofiira, kavalo mmodzi wakuda. Zitatu, zosiyana: zandale—mphamvu zandale, mphamvu yauzimu, zolamuliridwa ndi mphamvu ya ziwanda, imene ili yotsutsakhristu. Kusakaniza zonsezo pamodzi, ndipo inu muli nacho chotumbululuka, chinthu chowoneka modwala chimene iye akukwerapo. Kulondola. Tsopano zindikirani. Yang’anani chimene iye akukwerapo, wamawonekedwe-otumbululuka uyu, kavalo wamtundu-wotuwa, wosakanizika ndi kuda, kufiira, ndi kuyera; kubwera ku nkhondo, kusonkhanitsa omumvera ake kuchokera ku fuko lililonse pansi pa Kumwamba! Kodi Daniele sanamasulire loto, ndi kuwona nsempha wa chitsulo uwo ukuyenderera kulowa mu ufumu uliwonse, wa Roma? Apa iwo akubwera, akusonkhana.

Tsopano khalani phee potseka, miniti chabe, ndipo mverani mwatcheru.

³¹¹ Iwo akusonkhana mmenemo tsopano kudzachita izo, kubweretsa omumvera ake kuchokera ku ngodya zinai za dziko lapansi; akukwera kavalo wotumbululuka, wodwala, wamitundu-itatu, wosanganikirana. Munthu yemweyo!

³¹² Tsopano, mu Chivumbulutso 19, sikuti kokha iye akukonzekera, koma Khristu akukonzekera kukakomana naye iye. Nkhondo ikakhala yotentha ndi yamphamvu. Khristu, mu Chivumbulutso 19. Khristu wasonkhanitsa Ake, osati kuchokera ku ngodya zinai za dziko lapansi, chifukwa pakakhala otsalira pang’ono chabe. Akuchita chiyani Iye? Iye akuwasonkhanitsa iwo kuchokera ku ngodya zinai za Kumwamba. Ife tidzatenga iyo, “miyoyo ya pansi pa guwa,” mawa usiku, ndipo inu mudzawona ngati ziri zowona, kapena ayi. Ngodya zinai za Kumwamba; pa kavalo woyera ngati chipale!

³¹³ Iye ali nalonso Dzina, osati imfa, koma, “Mawu a Mulungu,” Moyo. Amen. Analilemba pa ntchafu Yake pomwe apa, “Mawu a Mulungu.” Ndiwo Moyo wokhawo, chifukwa Mulungu ali yekhayo gwero la Moyo Wamuyaya umene ulipo. Zoe! Kulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

³¹⁴ Ndipo Iye walilemba, “Moyo,” akukwera pa kavalo woyera; ndipo apa pali mwamuna ali nazo mphamvu zitatu zosiyana zosakanizikana, wotchedwa “Imfa.” Kusonkhanitsa nthumwi zake za pa dziko lapansi; ndipo Khristu akusonkhanitsa omumvera Ake obadwira-Kumwamba, oyera. Iye ali nayo “Imfa” italembedwa pa iye; Khristu ali nawo “Moyo” utalembdedwa pa Iye.

315 Iwo okhala naye Iye ali pa akavalo oyera, nawonso, ndipo iwo ali kutchedwa, “Osankhidwa maziko a dziko asanakhazikitsidwe.” Ameni! Ndipo iwo ali okhulupirika kwa Mawu. Ameni! Psyii! Ine ndikuchikonda chimenecho. “Akutchedwa, osankhidwa, maziko a dziko asanakhazikitsidwe.” Ndiyeno, wokhulupirika kwa Mawu, mwa kusankha kwawo, onse okondowedwa naye vinyo watsopano ndi Mafuta, akungokwera motsatira kumene, kubwera pansi kudzakumana naye iye. Iwo akudziwa Mabingu adzatitulutsira chinthu icho ife, posachedwa pompa. Mukuwona?

316 Yang’anani. Iye akuchita motani? Kotero, ngati Iye ali Mawu, ndipo, Dzina Lake liri Mawu, ndiye Mawu ali Moyo. Wotsutsakhristu; chirichonse cha *anti* chiri “chotsutsa,” kotero *anti* ali “kutsutsa” Khristu, Mawu. Kotero, chiyenera kukhala chikhulupiriro, kapena chipembedzo, chimene chiri chotsutsa Mawu.

317 Bwanji, ine sindikuwona momwe inu muti muphonyere icho. Ngati inu—inu mukumvetsa izo, inu mungachiphonye bwanji icho? Ine sindikudziwa momwe inu muti muchitire.

318 Ndipo izo nzowona. *Anti* ndiko “kutsutsa.” Kodi si kulondola uko? “Kuchotsapo.” Ndicho chimene iye anali. Iye akukwera kavalo wosanganikirana wake. Ife tikuwona izo pomwe apa mu Mawu a Mulungu.

319 Ife tinaziwona zimenezo komweko mu mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Apa Iye akuzibweretsanso izo kumene mu Zisindikizo, kuzitseguka ndi kuwonetsa zinthu izo zimene zinali kupitirira, pansi pa mibadwo ya mpingo.

320 *Anti* ndi “kutsutsa” Mawu. Mwawona chifukwa, zikhulupiriro, chifukwa chimene ife tiri otsutsa kwambiri zikhulupiriro ndi zipembedzo? Chifukwa izo zikutsutsa Mawu. Mukuwona?

321 Apa ife tikuwona Moyo ndi imfa zikubwera ku kulimbana kotsiriza. Kavalo woyera, wa Moyo wooka; kavalo- wotumbululuka, wa chikhulupiriro chosanganikirana. Iwo akuchiwona chinthu chikubwera ku—ku chiwonetsero chenicheni.

322 Tsopano ine ndikufuna kunena chinachake apa. Inu mukhoza kusakhulupirira ichi. Koma ine ndinachiyang’ana icho, kuti ndikhale wotsimikiza. Pali mtundu umodzi wokha wapachiyambi, ndipo ndiwo woyera. Ndi angati amadziwa izo? Pali mtundu umodzi wokha wapachiyambi. Wina uliwonse, uli wosakanizidwa.

323 Khristu ali pa Mawu olimba-oyera, osakhudzidwa, kuchokera pachiyambi. Ameni! Ameni! Mtundu uliwonse ukanakhala woyera ngati mankhwala ena akanapanda kuthiridwa mwa iwo. Ameni! Ulemerero! Mpingo uliwonse ukanamayima pa Chiphunzitso cha atumwi cha Mawu a

Mulungu, ndipo Mulungu nkumachitsimikizira Icho, ngati iye akanapanda kukhala nazo zikhulupiriro kapena zipembedzo zitasanganikirana kwa Icho. Ndi zimenezotu.

O, M'bale Evans, ine ndikumverera bwino pakali pano! Inde, bwana. Inde, bwana.

³²⁴ Mtundu umodzi wokha wapachiyambi, ndiwo woyera. Iwo suli—iwo sunasakanizikane nazo konse zipembedzo kapena zikhulupiriro. Ayi, bwana.

³²⁵ Ndipo, kumbukirani, oyera Ake avekedwa miinjira yoyera, osati yosakanizikana nazo zipembedzo ndi zikhulupiriro. Tsopano ife tikupeza, zikhulupiriro za chipembedzo, apa pali pamene inu mumatengera mtundu wanu wosanganikirana. Koma uwu uli mtundu wapachiyambi umene Iye akukwerapo. Mtundu wapachiyambi uli pa anthu Ake. Ndipo iwo aviikidwa mu Magazi, amene anatsuka chovala icho, ndi kuchitumiza icho mmbuyo kutsidya. Mukuwona? Uko nkulondola.

Iwo amene anasakaniza, anasanduka otumbululuka ndi kupita ku imfa.

³²⁶ Iko kuli kusokoneza, chisokonezo, kusakaniza mitundu ndi woyera; iwe umasokoneza mtundu wapachiyambi. Nkulondola uko? Ngati mtundu wapachiyambi, mtundu wokhawo, uli woyera, ndipo iwe ukusakaniza chinachake kwa iwo, iwe umasokoneza cholinga chake chenicheni. Amen. Nkulondola uko?

³²⁷ Ndipo, pamene, ngati Iye ali kavalo woyera, ndipo Iye ali Mawu; ndiye, kuti musakanize chirichonse ndi Iwo, chikhulupiriro cha mtundu uliwonse, kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo, kuchotsa Mawu amodzi kwa Iwo, ndiko kusokoneza chinthu chonsecho. O, mai! Ndisungeni ine ndi Mawu, Ambuye!

³²⁸ Chowonadi ndi cholakwika! O, mai! Ziribe kanthu kaya nzabwino bwanji kuti ziri... Chowonadi ndi cholakwika sizingasanganikirane. Izo sizingasanganikirane. Ndi mwina PAKUTI ATERO AMBUYE kapena ziri zolakwika. Ziribe kanthu kaya bambo woyera ati ananena izo, Bonifesi Woyera, kapena—kapena arikibishopu waku Canterbury; ine sindikudziwa amene ananena izo. Ngati izo ziri zosiyana kwa Mawu, ndi chisokonezo. Izo sizisanganikirana. Kutu, “Chifukwa, munthu uyu anachita...” Ine sindikusamala chimene iye anachita, kaya iye ali woyera kwambiri chotani, kapena chirichonse monga izo. *Ichi* chiri Chowonadi cholunjika chokha chimene ife tiri nacho. Palibe mpingo, palibe chikhulupiriro, chiribe Chowonadi, ngati icho chiri kunjira kwa *Ichi*.

³²⁹ Ndipo ndiwonetseni ine mmodzi amene ali nacho Icho. Basi, ine ndikufuna inu mudiwuzi ine. Ine nditsegula tsamba mu Baibulo, ndi kukuwonetsani inu chinachake. Mukuwona? Tchulani mmodzi yekha. Inu mukuti, “Chipentekoste.” O,

mai! Ine ndinangogwira lingaliro limenelo kuchokera kwa winawake apo. Ndicho chifukwa ine ndinanena izo. Kulibwino ndingochisiya icho chokha, pakali pano, chifukwa ine ndawona icho chinayamba malo achironda pomwepo. Ine sindinati—sindinafune kukupwetekani inu, koma ine—ine ndimangofuna inu mudziwe kuti ine ndikudziwa chimene inu mumaganiza. Mukuwona?

³³⁰ Iwo amene anasanganikirana, anakhala (anti) wa ku imfa. Iwo amakhala mtundu wa imfa, pamene iwe usakaniza mtundu uliwonse wa chirichonse ndi wapachiyambi.

³³¹ Izo ziri monga Khristu ananena za mbewu ya mpiru. Komabe, ndiyo yochepetsetsa ya mbewu zonse, koma siyidasanganikirana ndi chirichonse. Mpiru sudzasanganikira. Iye ali mpiru weniweni. Koteru ngati inu muli nacho chikhulupiriro chochuluka choncho, ingogwirani kwa icho.

³³² Zindikirani. Moyo unatsatira, wokwera pa kavalo woyera, Yemwe anali Mawu, Moyo, wotsimikiziridwa ndi oyera Ake owukitsidwa amene anali naye Iye. Tsopano nkondo iyenda motani?

³³³ Yesu anati, “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye anali wakufa, komabe iye adzakhala moyo.” Iye anati, “Ngati inu mukhulupirira mwa Ine, ngakhale inu—inu munali akufa, komabe inu mudzakhala moyo. Ndipo yense amene akhala moyo ndi kukhulupirira mwa Ine sadzafa konse.” Ndiponso, Iye anati, “Iye amene akhulupirira mwa Ine . . . Iye adzamupatsa iye Moyo Wamuyaya, kumuwukitsa iye pa masiku otsiriza.” Ndilo Lemba Lake lolonjezedwa.

³³⁴ Apa pakubwera Satana, ndi ngodya zonse zinai za dziko lapansi, ndi Aprotestanti ake ndi ake—Akatolika ake, ndipo onse pamodzi, kuguba chamtsogolo kupita ku Nkhondo ya Armagedoni. Chabwino.

³³⁵ Ndipo apa pakubwera Yesu, kubwera pansu kuchokera Kumwamba, ndi oyera owukitsidwa, Mawu otsimikiziridwa.

³³⁶ Ine ndinati, ngati Mulungu alankhula, kapena kukutumani inu, Iye ali . . . Iye—Iye amayikira kumbuyo chimene iwe ulankhula. Mukuwona? Zindikirani, ngati iwe uli kazembe wochokera Kumwamba, Kumwamba konse kuli kumbuyo kwako. Ndipo Kumwamba kuli kodzaza Mawu. A-ha.

³³⁷ Zindikirani, tsopano, Iye akubwera nawo oyera owukitsidwa, kutsimikizira kuti Mawu Ake ali owona.

³³⁸ Koteru Satana akudziwa, ndiye, maphompho opanda malire akonzedwera iye. Mukuwona? O, mai! Pamene, imfa inakwera kavalo wotumbululuka, wosakanizika chikhulupiriro ndi zipembedzo, ndi kumutsatira iye, o, mai, ku kulekanitsidwa Mwamuyaya kuchokera kwa Mulungu. Ndiko kumene iye anakwera nawo, ku kulekanitsidwa Mwamuyaya.

Khristu anakwera Mpingo Wake kulowa mpaka mu Ulemerero, mu chiwukitsiro.

339 Zindikirani ndime 8 tsopano, basi mpaka . . . gawo lotsiriza la ndime 8, pamene ife tikutseka, onani.

. . . *mphamvu inapatsidwa kwa iwo* . . .

340 Ndi ndani “iwo”? Mukuwona? Chabwino. Wotsutsakhristu, wotchedwa “Imfa.” “Gehena inatsatira.” Yang’anani kachitidwe kake ka nsonga zinai.

341 Wotsutsakhristu, kavalo woyera; amapha mwa mzimu, pokhala wotsutsakhristu; kupha mwauzimu.

342 Wachiwiri, kavalo wofiira; amapha mwa lupanga; mphamvu za ndale, pamene mpingo ndi dziko zinalumikizana.

343 Kavalo wakuda; miyoyo, pamene iye anapereka chiphunzitso chake, ndipo iye anachita kumeneko ndi ziwerewere zake. Ndipo iye ankayeza chakudya chawo ndi . . . kugulitsa chawo . . . zimene iwo ankapereka kukhala chakudya, kwa muyezo, ndi marupiya, ndi zina zotero.

344 Wachinayi, kavalo wotumbululuka; kulekanitsidwa Mwamuyaya kuchoka kwa Mulungu. Kachiwiri, anai, mwawona. O, mai!

Mulungu alemekzedwe!

345 Tsopano, wotsiriza, apa mu kutseka. Kwa iwo . . . Kodi inu muli nayo . . . Ine ndikudutsitsa nthawi, koma kodi inu mungandipatse ine pafupi maminiti ena khumi? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ine ndiri nako kuyitana kochuluka, lero, kwa—kwa kuti ine ndilankhule apa.

346 Pakhala pali zotentheka zambiri zomwe zayamba, za Eliya, mpaka izo zangokhala . . . Izo—izo zakhomeredwa ku imfa. Ndipo inu mukhoza . . . Chabwino, mungolola . . . Chabe Mulungu atandithandiza ine kuti ndikuthandizeni inu kuti muwone chimene ine ndikuyang’anapo. Kodi inu mutero? Tiyeni tingoyesa kutero, onani.

347 Tsopano apa pali, mu kutseka, kwa iwo amene sakhulupirira kuti mtumiki wotsiriza ku m’badwo wa mpingo ndi Eliya mneneri, mwamuna wodzozedwa mwa mzere umenewo.

348 Itachitika imfa . . . Yang’anani. Itachitika imfa, ya m’badwo wotsiriza uwu . . . Tsopano, inu mukuzindikira chimene chinachitika, taonani. Itachitika imfa, matupi awo akufa akuwonongedwa ndi zirombo zolusa. Inu mukudziwa zimenezo. Tsopano, izo nzowona. Monga wawo, anali naye woyimira wa Yezebeli.

349 Tsopano tsegulani ku Chivumbulutso 2:18 ndi 20. Ine ndikukhulupirira tinapeza apo maminiti pang’ono okha apitawo. Sichoncho? Eya, ine ndikukhulupirira ife tinapeza kumene apo. Ine ndinali nazo izo nditawalemba apa

ena... Inde. Nthawi ya kuvunda kwa khalidwe, ndicho chimene icho chinali. Onani momwe izo zinali, momwe Yezebeli anabwereramo. Tsopano, Yezebeli ali mipingo, mpingo wamakono uwu; osati Mkwatibwi, tsopano. Yezebeli, mu Chipanganano Chakale, ali choyimira cha mpingo lero, malingana ndi Mawu a Mulungu, a Chivumbulutso 2:18, 20.

... iwe ukulola mkazi uja Yezebeli, yemwe anadzitcha yekha mneneri wamkazi, . . .

³⁵⁰ Mukuwona? Kodi nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, izo zikuyimira mwangwirowo kwa Yezebeli. Tsopano, choyamba . . .

³⁵¹ Ife tikhoza kungokupatsani inu Lemba pambuyo pa Lemba, mwawona, kuti m’badwo wotsiriza uli Uthenga wa uneneri kwa Mpingo, kuwayitana iwo kuti abwerere ku Mawu apachiyambi. Tsopano zindikirani. Kodi uko nkulondola? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Malaki 4 ananena choncho, ndi ena, Chivumbulutso 10: 7, ndipo mpakabe mmusi. Mukuwona? Yesu Mwiniwake ananeneratu zimenezo, mmusi, mmusi, mmusi. “Monga izo zinaliri mu masiku a Loti,” ndi zina zotero monga choncho, ndipo mpaka mmusi. Izo zikumangobwerabe mpaka mmusi.

³⁵² Yezebeli ali choyimira cha mpingo wamakono lero chifukwa Akatolika ndi Aprotostanti ali olumikizana pamodzi tsopano. Apo—apo palibenso kulambalala chimenecho. Iwo onse ali zipembedzo, kotero ziri chabe—ziri chabe mayi ndi mlongo, ndicho chonse. Iwo amakangana ndi kutsutsana wina ndi mzake, koma iwo ali chinthu chomwecho, onsewo timahule. Tsopano, ine sindikunena zimenezo ndekha. Ine ndikutenga kuchokera ku PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuwona? Chabwino.

³⁵³ Tsopano ife tikuzindikira, anaphedwa mwa kulamulira kwa Mulungu, anali Yezebeli, anaphedwa chifukwa Mulungu anali naye Jehu kuti apite kumusi uko ndi kukamuponyera iye kunja pa zenera, ndi kumupha Yezebeli. Ndipo agalu nkudya thupi lake, (nkulondola uko?) Yezebeli weniweni. [Osonkhana anati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ahabu, mfumu yake, mutu; agalu ananyambita magazi ake, monga Eliya woyamba ananeneratu. Mukuwona kumene ife tikupita, si choncho inu?

³⁵⁴ Chifukwa? Eliya woyamba anali mwamuna wokanidwa, ndi mipingo. Ndipo Yezebeli ndi Ahabu anali mitu ya mipingo imeneyo, mpingo ndi dziko, zonse pamodzi. Ndipo Elisha anawulula machimo a Ahabu kwa iye, ndipo analamulira mpingo wonse kuti ubwerere ku Mawu owona.

³⁵⁵ Ngati izo siziri chimodzimodzi zimene Eliya wachiwiri ayenera kuchita pamene iye akubwera ku mpingo uwu mu tsiku lino, “kubwezeretsanso Chikhulupiro chapachiyambi”! Ine sindikudziwa momwe inu muti muthawire kwa Iwo. Uko nkulondola. Bwererani ku Mawu owona! Uko nkulondola.

356 Tsopano ngati inu mukufuna kuwona matupi awo, tiyeni titsegule apa ku Chivumbulutso 19, atatha—atatha Mawu kuwadula iwo. Tsopano, Mawu akawapha iwo. Inu mukudziwa zimenezo. Chabwino. Tsopano inu mungoyang’ana ndi kuwona chimene chikuchitika pamene Khristu Akubwera, mu Chivumbulutso 19, kuyambira ndi ndime ya 17.

Ndipo ine ndinawona mngelo alikuima mu dzuwa; . . .

357 Tsopano, ndizo zitachitika kumene, yang’anani pamwamba apa, “Ndipo chovala Chake chinali chitamizidwa nawo magazi. Ndipo Iye ali akutchedwa MFUMU YA MFUMU, NDI MBUYE WA MBUYE.” Mu ndime ya 13, “Iye akutchedwa Mawu a Mulungu.” Mukuwona? Tsopano, apa Iye ali, “MFUMU YA MFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE.

Ndipo ine ndinawona mngelo . . .

358 Tsopano yang’anani. Iye akupitirira.

Ndipo kuchokera mkamwa mwake mukutuluka lupanga lakuthwa, kuti ndi ilo iye akakanthe mafuko: . . .

359 “Kuchokera mkamwa Mwake,” monga kuchokera mkamwa mwa Mulungu kupita ku kamwa ya Mose. Mukuwona?

. . .ndipo iye adzawalamulira iwo nayo ndodo ya chitsulo: ndi..kuponda moponderamo mphesa—moponderamo mwa ukali ndi mkwiyo wa Mulungu Wamphamvuzonse.

Ndipo iye ali nalo pa chovala chake dzina..pa ntchafu yake dzina lolembedwa, MFUMU YA MFUMU, NDI MBUYE WA AMBUYE..

Ndipo ine ndinawona mngelo . . .

360 Tsopano yang’anani. Tsopano Iye akutulukira, akukantha. Iye akumukantha ndani? Yezebeli ndi Ahabu wake, mneneri wabodza.

Ndipo ine ndinawona mngelo alikuyima mu dzuwa; ndipo iye analira ndi liwu lokweza, kunena kwa mbalame zonse za mu mlengalenga mkati mwa miyamba, Bwerani ndipo dzisonkhanitseni nokha limodzi ku mgonero wa Mulungu wamkulu;

361 Iye akuwadyetsa iwo kwa zirombo ndi mbalame. Tsopano yang’anani cha apa mu mutu wina apa, wa Bukhu la Chivumbulutso. Ndipo, miniti yokha, “Kupha ndi lupanga, ndi imfa, ndi zirombo za dziko lapansi.” Mukuwona? Mpingo wa Yezebeli, thupi lake (lenileni), liri lakuti lidyedwe ndi mbalame ndi zirombo za padziko lapansi. Chimodzimodzi basi monga Ahabu ndi Yezebeli analiri, mwa chirengedwe, koteri iwo ali oti atero, mwa mawonekedwe auzimu, mpingo. Kodi

inu mukuwona chimene ine ndikutanthawuza? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino.

³⁶² Eliya...O! Eliya anali mneneri mu masiku a Ahabu ndi Yezebeli, mwachibadwa. Ndipo iye walonjezedwa kuti achita chinthu chomwecho, molingana ndi PAKUTI ATERO AMBUYE, mu Mawu, kwa Yezebeli, mwauzimu; utumiki wake wamawonekedwe—Auzimu.

³⁶³ Yang’anani. Eliya, ngakhale, mu tsiku lake, bwinobwino ndi mwakuya anatsimikizidwira, sakanakhoza kuwatembenuza iwo kubwerera ku Mawu. Nkulondola uko? Ngakhale, Eliya anayesera, ndi chirichonse. Iye anachita chirichonse. Iye—iye anawawonetsa iwo zizindikiro ndi zodabwitsa; ndipo iwo anaseka pa nkhope yake. Chinthu chomwecho iwo adzachita ndi wauzimu apa, mwawona. Iye sakanakhoza kuwatembenuza iwo kubwerera ku Mawu. Kuchokera mu mamiloni . . .

³⁶⁴ Tsopano mverani, mpingo, kutseka tsopano, inu amene muli osokonezeka pang’ono pa izi.

³⁶⁵ Kuchokera mu mamiloni mu dziko, mu masiku a Eliya, pamene Yezebeli ndi Ahabu ankalamulira, mwa—mwa choyimira cha chenicheni lero; kuchokera mu dziko lonse, uko kunali mazana asanu ndi awiri okha opulumutsidwa, a kulalikira kwa Eliya. Nkulondola uko? Ndizo chimodzimodzi.

³⁶⁶ Penyani, Eliya sanadziwe konse ngakhale mmodzi wa iwo anali choncho. Iye ankalingalira kuti anali mmodzi yekha wopulumutsidwa, mpaka Mulungu anatsegula chimodzi cha Zisindikizo ndipo anawawonetsa iye chinsinsi mu Bukhu, kuti Iye anali nawo mazana asanu ndi awiri amene sanalambire konse kwa zikhulupiriro zimenezo zomwe iwo anali nazo. Pamene Mulungu anatsegula Bukhu Lake kwa Eliya, anati, “Tsopano dikira miniti, mwana. Ine ndiri nawo mazana asanu ndi awiri amene alipo, ali kumeneko, ali nawo maina awo pa Bukhu ku maziko a dziko. Iwo ali Anga.” Psyii! Mulungu anatsegula Zisindikizo.

³⁶⁷ Ndicho chifukwa chake ine ndikuganiza Yohane anali kuchita kufuwula mochuluka usiku wina. Iye ayenera kuti analiwona dzina lake Pamenepo, inu mukuwona. Mwawona?

Tsiku limodzi Mulungu anatsegula . . .

³⁶⁸ Elisha, iye anali atalalikira. Iye anali atachita chirichonse, ndipo—ndipo—ndipo analalikira mtima wake panja. Iye anali atachita chirichonse iye akanatha, ndipo komabe iwo basi “ankamukuwa” iye, kumutcha iye chirichonse, ndipo anati, “Iwe ndiwe chiyambi cha zonse izi. Iwe ndiwe wamizimu. Iwe ndiwe mmodzi amene ukupangitsa vuto lonse kuti libwere. Iwe ndiwe wolakwa,” ndi chirichonse monga izo. Iye ananena chirichonse kwa iye. Yezebeli anawopsyeza kuti awudula mutu wake, ndi china chirichonse. Uko nkulondola. Aliyense anali kumutsutsa iye.

369 Ndiyeno iye anati, “Ambuye, ine nditatha kuchita izo, zonse zimene Inu munandiwuza ine kuti ndichite! Ine ndakhala nawo chimodzimodzi Mawu Anu. Pamene Inu munandiwuza ine chirichonse, ine ndinalibe mantha. Ine ndinayenda mpaka pamaso pomwe pa mfumu, ndi china chirichonse, ndi kuwawuza iwo, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE.’ Ndipo Inu simunandiwuze ine kanthu, ndipo ine sindinawawuze iwo kanthu kamodzi, koma chimene chinachitika. Ndipo tsopano ine ndiri pano, mmodzi yekha amene watsala, kuchokera mu gulu lonse. Ine ndine mmodzi yekha amene watsala, ndipo iwo akuyesa kundipha ine.”

370 Mulungu anati, “Ine nditsegula chimodzi cha Zisindikizo ndi kukuwonetsa iwe chinachake.” Iye anati, “Iwe ukudziwa, ine ndiri nawo mazana asanu ndi awiri kumbuyo uko, amene sanagwadirepo bondo kuti... kujowina chirichonse cha zikhulupiriro zimenezo panobe, zipembedzo. Alipo mazana asanu ndi awiri a iwo okonzekera Mkwatulo, mwawona.” O! O! Iye ananena kwa mneneri Wake, yemwe Iye amawululirako Mawu Ake, mwawona, kupyolera mu Lemba. “Ine ndiri nawo mazana asanu ndi awiri maina okonzeka panobe, kuchokera mu m’badwo uwu; mazana asanu ndi awiri a iwo. Iwo sanagwadire mawondo awo kwa aliyense” (ngati ine ndinganene izi mu tsiku lino) “zipembedzo za mabungwe, ndi kubwera mwazikhulupiriro, mkati mwawo.”

371 Inu mukuwona chimene ine ndikutanthawuza? Ndiye, mophweka icho chiyenera kukhala. Icho basi chiyenera kukhala. Ndipo chiri molingana ndi Mawu. Pamene munthuyu afika powonekera, iye adzakhala mneneri. Motsimikiza basi monga mwene ine ndikuyimira pa guwa ili. Mukuwona? Ndipo iye adzakhala nawo kumene Mawu amenewo. Iye sadzatengera chikhulupiriro cha aliyense kapena china chirichonse. Uko nkhulondola. Iye adzakhala munthuwamtchire munthu wa mtundu umenewo, monga Elisha anali, iye... ndipo monga Yohane anabwera. Iye adza—iye adzadana nawo akazi, (mnyamata!) akazi amakhalidwe oyipa! Psyii! Mnyamata, iye adzawanda pa iwo! Eliya anachita, chonchonso anachita Yohane. Mukuwona? Mukuwona? Ndipo iye adzakhala mowongoka choncho nawo Mawu amenewo. Iye adzakhala—adzakhala wotsutsa mabungwe. Bungwe? “Musaganize zonena mwa inu eni, ‘Ife tiri naye Abrahamu monga atate athu,’ pakuti ine ndikuti Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.” Mukuwona? Ndithu anachita.

372 Tsopano, ndi zimenezotu, amzanga. Apa pali Chisindikizo Chachinai, chitatsegulidwa. Ndiponso okwera a akavalo anai awululidwa, mwa kukhoza kwa kudziwa kwanga. Tsopano, izi ziri zonse zimene zinachitika pa dziko lapansi.

373 Chisindikizo chotsatira, ife tikuwona, chiri Kumwamba, pamene miyoyo ili pansu pa guwa.

374 Tsopano, mwa kutseka chabe, ine ndikufuna kulankhula ziwiri izi. . . mawu pang'ono chabe, pomwe apa, amene ine ndawalemba. Ife talumphapafupi, pa Zisindikizo zinai izi, Zisindikizo zinai zoyamba.

375 Tsopano, mawa usiku, ife—ife tisintha malo, kuchokera pazinthu za padziko lapansi kupita patsogolo. Iye akuyang'ana mmwamba apa ndi kuwona miyoyo ya pansipansi pa guwa, yochitidwa nsembe, guwa.

Usiku wotsatira, chiweruzo chikukantha.

376 Ndipo usiku wachinai, kapena usiku wotsiriza, Lamlungu usiku, ine sindikudziwa chiyani. Ine sindikudziwa chomwe zina izi zikutanthawuza. Ine ndinangowerenga izo, monga inu munachitira. Koma, “Uko kunali chete kwa theka la ora,” koma pali chinachake chimene chinachitika. Ine ndikumuyembekeza Iye kuti awulule Icho. Iye adzachita izo. Ine ndiri wokhutitsidwa Iye adzatero.

377 Ife tinachita kupita, mu malo osiyana a Lemba, ku Chivumbulutso 19, kuti tiwonetse Kubwera kwa Khristu kudzapha wotsutsakhristu. Ndicho chifukwa chake ine ndinachita kusiya izi, kungotenga ndime ziwirizo. Ine ndimayenera kupita ku zigawo zosiyana za Malemba, kukatsimikizira zinthu izi. Kotero ndicho chifukwa ine ndinapita ku Chivumbulutso 19, kuti ndiwonetse mapeto a wotsutsakhristu, adzakhala kupha; kwa Khristu, pamene Iye akubwera, Iye adzapha wotsutsakhristu.

378 Ku Chivumbulutso 10, kuti tiwonetse kuti Uthenga wa mngelo wachisanu ndi chiwiri adzakhala munthu, mu masiku ano otsiriza, wodzozedwa ndi Mulungu kwa utumiki monga ngati Eliya mneneri ali, monga zaneneredweratu mu Malaki 4, kuti awulule Mawu owona a (pachiyambi) Mulungu mu m'badwo uno, Mawu apachiyambi a Mulungu mu m'badwo uno. Monga iye anachitira kwa Yezebeli wachibadwa, kotero munthu uyu adzachita icho kwa Yezebeli wauzimu, mipingo yachipembedzo. Ine ndinachita kupita ku mutu wa 7. . . mutu wa 10, ndime 1 mpaka 7, kuti nditsimikizire kuti zinali zolondola. Ndipo uko ku Malaki, ndi Amosi, ndi ena otero, kuti nditsimikizire izo.

379 Eliya anali mneneri amene ananenera ndi kudzudzula Yezebeli, mu m'badwo umenewo wokha.

380 Ndipo Eliya sanafe konse. Iye ndithudi sanatero. Iye anawonekera kachiwiri, zaka zina mazana asanu ndi atatu mtsogolo, pa mbali ya Yesu Khristu, pa Phiri la Chiwalitsiro. Iye sali wakufa.

381 Tsopano, ife tikupeza kuti Mzimu wake uli woti udzozo munthu, malingana ndi lonjezo la Mulungu, mu masiku otsiriza; analonjeza kuchita zomwezo mwa Yezebeli wauzimu, monga zinachitira mwa Yezebeli wachibadwa, mu m'badwo wotsiriza.

³⁸² Ndicho chifukwa ine—ine ndinapita ku zambiri chotero za Baibulo, kuti nditsimikizire zimenezo, kotero izo sizitsalira funso mu maganizo anu. Ngati liripo, inu mundidziwitse ine. Chabwino, mundilembere ine kalata kapena kapepala kakang’ono.

³⁸³ Ndipo izo mwangwiro zikugwirizana, ngakhale ku zirombo kuwononga matupi awo achibadwa mu tsiku lotsiriza, kuwawononga iwo monga anachitira nthawiyo.

³⁸⁴ Mwa kukhoza konse kwa vumbulutso langa, limene linapatsidwa kwa ine ndi Mulungu ndipo ananeneratu kuti zidzachitidwa, ichi chiri Chowonadi cha okwera pa kavalo anai, mwa kukhoza konse kumene ine ndikudziwa.

³⁸⁵ Inu mukuganiza chiyani za Yesu? [Osonkhana akusangalala—Mkonzi.]

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nagula chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

³⁸⁶ Tsopano kumbukirani, wopanda . . . (Ndi choncho; pitirirani; ndizo zabwino.) Popanda malingaliro oipa pa anthu aliwonse mu bungwe lirilonse! Chifukwa, Mulungu ali nawo ana mu kachitidwe ka Chikatolika. Iye ali nawo ana mu kachitidwe ka Chimethodisti. Iye ali nawo ana mu kachitidwe ka Chibapatisti. Ndi angati a iwo, iwo onse machitidwe osiyana, ali kuyimiridwa pano usiku uno, amene anatuluka kuchokera mmenemo pamene inu munawona Kuwala? Tiyeni tiwone manja anu. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, kumbukirani, kuli anthu kunjako monga ngati inu. Koma ndi kachitidweko kamene kamapha, mwawona. Ndiwo mzimu wotsutsakhristu umene potsiriza umawatengera iwo ku malo mpaka sadzamvanso Chowonadi.

³⁸⁷ Ndipo mukukumbukira usiku wina, pamene ine ndinkadutsa kupyola mu kusindikiza? Ngati munthu anamva kuyitana kwa chisangalalo, ndipo iye anakana kupita ali mfulu, iye amatengedwera ku mtengo ndipo chiwuzilo chimabowola khutu lake. Khutu ndiko kumene iwe umamvera. “Ndipo chikhulupiriro chimadza pa kumva.” Ndiye ngati iye amva Iwo, ndipo nkukana kuvomera ufulu wake, ndiye iye ali . . . ayenera kutumikira bwana wake wa chipembedzo kwa moyo wake wonse. Amenii.

³⁸⁸ O! O, mai! Kodi sali Iye wodabwitsa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

Ndimkonda Iye, ndi . . .

Tiyeni tingokweza manja athu tsopano ndi kumpembedza Iye.

Poti Iye anayamba kundikonda (Ulemerero!)
 Nagula chipulumutso changa
 Pa mtengo wa Kalvare.

³⁸⁹ [M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Ndimkonda Iye*—Mkonzi.] Tsopano ingoweramitsani mutu wanu, ndipo tiyeni timupembedze Iye tsopano pamene ife tikung'ung'uza iyo. [M'bale Branham akupitiriza kung'ung'uza *Ndimkonda Iye*.]

³⁹⁰ Ambuye, tiri othokoza bwanji ife! Ine ndiri wokondwa kwambiri, Ambuye, wokondwa kwambiri chifukwa cha Inu ndi anthu Anu. O Ambuye, Inu munagula chipulumutso chathu pa Kalvare. Ife tikulandira mokondwa icho, Ambuye.

³⁹¹ Tsopano tiyeseni ife, Ambuye, mwa Mzimu Wanu. Ndipo ngati pangakhale choyipa chirichonse pakati pathu, Ambuye, kusakhulupirira kulikonse kwa Mawu, munthu aliyense muno, Atate, amene sakanavomereza lonjezo lililonse la Mulungu ndi “ameni”; Mzimu Woyera utabwera pansu tsopano, Wokwera kavalo woyera, pamene Mzimu Wake, Mzimu wa Khristu pamaso pa wotsutsakhristu, ndi kuyitana a Iye Mwini. Ayitanireni iwo kunja, Ambuye.

³⁹² Tsopano iwo atalapa, abwere mwamsangaa kwa Inu ndi kudzazidwa nawo Mafuta ndi vinyo; ndi kusinthidwa kuchokera ku mwinjiro wa chipembedzo uwo wa imfa ya Kaini, kupita ku mwinjiro woyera ngati chipale cha Moyo Wamuyaya, woperekedwa ndi Mkwati. Ndiyeno iwo adzapita ku Mgonero wa Chikwati tsiku lina, mu Mawu otsimikiziridwa a chiwukitsiro. Perekani izo, Ambuye. Fufuzani mitima, pamene anthu akuyembekezera pa Inu. Kupyolera mu Dzina la Yesu!

[M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Ndimkonda Iye*—Mkonzi.]

³⁹³ Tsopano, mungofufuza mtima wanu, m'bale wanga, mlongo wanga, mzanga. Ine ndakhala ndi inu nthawi yayitali. Izi ziri pafupi zaka makumi atatu ndi zitatu. Kodi ine ndinayamba ndakuwuzani inu chirichonse mu Dzina la Ambuye chimene sichinadzachitike? [Osonkhana ati, “Ayi.”—Mkonzi] Fufuzani Khristu tsopano pamene inu muli nawo mwayi wotero. Izo zikhoza kubwera posachedwa pompa pamene inu simungakhoze kuchita icho. Mukuwona? Iye akhoza kusiya mpando, nthawi iliyonse, wa chitetezero Chake; ndiye inu mukhoza kulira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kupondaponda, inu mukhoza kulankhula mu malirime, inu mukhoza kuthamanga uku ndi uku pansu, inu mukhoza kuchita chirichonse chimene inu mungafune kutero, ndi kujowina mpingo uliwonse mu dziko, palibe chirichonse, palibenso bulitchi ya lanu—ya tchimo lanu. Ndiye inu muchita chiyani, inu muli pati ndiye?


³⁹⁴ Chabwino, ine ndikukhulupirira, ndi mtima wanga wonse, mpando uli wotsegulabe. Ine ndikukhulupirira Iye akadali pa Mpandowachifumu wa Mulungu. Koma posachedwapa

Iye awuka tsopano, ndi kutulukira, kudzatenga zomwe Iye waziwombola. Iye akuchita ntchito ya Wowombola Wachibale, pamene Rute akuyembekezera.

³⁹⁵ Koma posachedwa, inu mukudziwa, Boazi atachita ntchito ya wachibale, ndiye iye akubwera ndi kutenga zomwe ziri zake. Ndipo ndicho chimodzimodzi chimene Baibulo linati Iye anachita, “Iye anatulukira ndipo anatenga Bukhu.” Ndiye chitetezero chatha; Iye wachokapo pa Mpandowachifumu; palibenso Magazi pa Mpando Wachifundo. Ndiyeno ndi chiyani icho? Mpando Wachiweruzo.

³⁹⁶ Musalole kuti zidzalankhulidwe, ena a masiku awa, “Ine ndimaganiza Mkwatulo umayenera kubwera.” Ndi kumva Liwu likunena, moyankha, “Zachitika kale.” Mulungu akuthandizeni inu!

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu.

³⁹⁷ M'bale Neville, bwerani, kuti mutibalalitse kapena chirichonse chimene inu muyenera kuchita. Mulungu akudalitseni inu, mpaka mawa usiku. 

CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©1994 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org